


MALO OKHAWO OPEREKEDWA

NDI MULUNGU OPEMBEDZERAPO

 Mmawa wabwino! Wokondwa kukhala pano mmawa uno. Ndipo ndife okondwa, tikusangalala ndi chiyanjano chachikulu ichi mozungulira nyimbo zakale izi za chikhulupiriro. Ife tikuzikonda izo. Sichoncho inu? Kolasi ya *Ameni*. Ndicho chimene Iye ali, *Ameni*, mwaona. Iye amakhala ndi mawu omaliza oti anene.

² Ine ndinali nditakhala pamenepo ndikuyankhulana ndi mzanga wakale, M'bale Brown, pamene nyimbo zimapitirira. Ndipo iye anati, "M'bale Branham, ine ndinali ndisanawone kufikira dzulo, chimene inu mwakhala mukuchikamba." Iye anati, "Ngati anthu atangolowa mu chimene inu mukukamba," anati, "chotchinga chirichonse chikanachoka pa njira." Ndiko kulondola ndendende. Ndiko kulondola. Ndiko kulondola ndendende. Ngati inu mukanangochimvetsetsa Icho, mukanachigwira Icho. Mukuona?

³ Ndikuyankhulana ndi mzanga wamng'ono, Ernie Fandler. Ine ndikuganiza ena a inu kunja uko pa zolumikiza mumukumbukira Ernie, momwe iye anatembenezidwira, momwe iye anatsogoleredwera kwa Ambuye. Iye samayankhula Chingerezi chabwino, kapena ndikanafuna kuti iye abwere adzanene mawu. Ndipo iye amasokoneza ma *we* ake ndi ma *W*. Iye amandifunsa ngati ndikuikumbukira nthawiyo, kunali ku Shawano, kumene iye amakhala. Bambo anafera mu msonkhano momwemo, anagwa pa mpando wake nkufa, wa Lutheran. Tinapangitsa aliyense kukhala chete. Ndinayankhula Mawu a Ambuye pa iye, iye anabwerera ku moyo, ndipo anabwerera ku ntchito. Um-hum. Iwo sanaiwale konse zimenezo, akufuna kuti ife tidzabwererenso.

⁴ Ine ndinamva kuti ku France, mmawa uno, kuli abwino kuposa anthu thuu sauzande achi French pa kusala kwa masiku angapo, kuti ife tidzapite kukabweretsa Uthenga ku France, mu France, fuko lonselo la Chiprotestanti, gawo la Chiprotestanti la fuko la France. Ndipo chotero ife tiri. . .

⁵ Zangoyamba kuyanga tsopano, zikuyamba kumene, mankhusu akukanganukapo kuti tirigu athe kukagona panja apo tsopano. Mukuona? Chotero mungokhala molemekeza, muzingopitirira kumapemphera. Mukuona? Kumbukirani, "Iwo amene ayembekezera pa Ambuye, adzawonjezera mphamvu zawo."

⁶ Tsopano, pali...Ine ndinali...kukalamba kwenikweni, ndipo ndinaganiza, “Kodi ine...Kodi padzakhalanso chitsitsimutso china, ine ndidzachiwone nthawi yina?” Ndipo mungokumbukira, kuchokera kumadzulo kudzabwera wokwera pa kavalo woyera. Tidzayendanso mkanjiraka kachiwiri. Izo nzoona. Posachedwapa tikadzati takonzeka. Ndi lonjezo, inu mwaona.

⁷ Tsopano, ine ndikufuna kunena kwa M’bale Leo...Ine ndimakamba za M’bale Wood usiku wathawu, mchimwene wake alikuno. M’bale Leo, ngati iwe ndi gulu laling’ono limene lalumikiza uko mmawa uno; Mlongo Mercier, abambo anu ali kuno. Ine ndinawawona iwo usiku wathawu. Iye ali kozungulira kuno mchipindachi penapake, ndipo iye akuwoneka bwino ndiponso akukongola.

⁸ Mmawa umene iye anachiritsidwa ku kachisi, panali matenda awiri akuluakulu a khansa, akufa kwenikweni, ndipo awiri onsewo anachiritsidwa. Ndipo bambo ake, bambo wachikulire ali ndi vuto la mtima, anatulutsidwa ku ulemelero wa Mulungu. Ndipo iye ali mu msonkhano kuno penapake. Ine sindikutha kumuwona iye pakati pa gululi tsopano, koma iye anali pano usiku wathawu.

⁹ Moni kwa inu nonse kunja uko kudutsa mdzikoli; kuno pamalo odabwitsa awa, a Life Tabernacle kuno ku Shreveport, ndi chigulu chothithikana kamba ka Sande sukulu. Inu mukudziwa, ngati ine ndikanamakhala ku Shreveport, osati kuti ndikunena kanthu komutsutsa aliyense, koma ano angakhale malo amene ine ndikanamabwera ku tchalitchi, komwe kuno ku Life Tabernacle. Ichi si chipembedzo. Life Tabernacle, lero, ndi kachisi wa zipembedzo zosiyanasiyana. Iwo anatulukuka mu chipembedzo chifukwa anandilandira ine ndi Uthenga uwu umene ine ndikulalikira. M’bale Jack Moore, m’bale wanga ndi mzanga, iye anachotsedwa kuchokera ku chipembedzo chifukwa iye amayanjana ndi ine. Ndipo chotero ine ndikuganiza iye akuyenera kuyamikiridwa. Izo nzoona. Mulungu amudalitse iye. Ndipo tizigwira manja ake mu pemphero, ndi kukhulupirira ndi iye.

¹⁰ Ndipo tsopano Mlongo Moore, ine sindikumuona iye paliponse, iye, inde, kumbuyo kuno, iye akuwoneka ngati mtsikana wamng’ono wakhala apo mmawa uno, yense wavala motere, mwatsopano, mu ichi, zikuwoneka ngati chovala cha Isitara. Ndipo izo zikuwoneka...M’bale Jack samamudziwa nkomwe iyemwini. Tsopano, tsopano Mlongo Moore!

¹¹ Ife ndithudi tikumusowa Anna Jeanne ndi Don, ndi onse a iwo. Ndine wokondwa kukumana ndi M’bale Nolan, a... mmodzi wa othandizana nawo pano.

¹² Ndipo M’bale Ernie, ine ndinamufunsa iye dzulo ngati iye angayimbe *Ameni* uja. Ine ndiri nayo iyo pa rekodi,

ndipo ndachitopetsa chinthucho pomangoimvetsera iyo mobwerezabwereza, *Ameni*. Ine ndikuganiza iye ali ndi liwu la iyo; amawaposa aliwonse a iwo. Ndipo Judy wamng'ono, ine ndinamuzindikira iye; awiriwo, amangowoneka basi ngati mchimwene ndi mchemwali. Sichoncho iwo? Iwo ndi mwamuna ndi mkazi. Tayang'anani pa aliyense wa iwo, mwaona, bwanji iwo akungowoneka ndendende. Mukuona? Ndipo kwenikweni banja laling'ono lokondana. Ndizo, inu mukudziwa, ndizo. . . M'bale Palmer amene wangokwera kumene makwerero agolide, ameneyo ndi mwana wake wamkazi ndi mpongozi wake wamwamuna. Ndipo ndizo. . .Iye ndithudi ndi wothandiza kwambiri pa kuphunzitsa kwake kwabwino kwa mwana. Ndipo ali nawo ena aponso, azitumiki okwatira nawonso, ndipo awa ndi avangeri ndipo ali ku munda kwawo, ndi ena. Chotero ndi zopambana basi.

¹³ Ine sindinamuwone Mlongo Palmer. Kwenikweni, ine sindikudziwa ngati ine ndingamudziwe iye ngati ine nditamuwona iye, kapena ayi. Iye ndi, mwinamwake, penapake (ndithudi) mu msonkhano. Mmbuyo kumbuyo uko; Mulungu akudalitseni inu, Mlongo Palmer.

¹⁴ Mtima wanga umanjenjemera nthawi zonse ndikaganiza za izo. M'bale Palmer anali atangokwera masitepe koma maminiti pang'ono, kufikira nditalandira uthenga wakuti iye wapita. Ine basi sindinakhulupirire izo. Billy anandiyimbira ine, ndipo winawake anali atagwira. . .ndipo iwo anadziwa. Iye tinali abwenzi okondana chomwecho, ndipo kudzadziwa kuti iye wapita, zinali zonjenjemeretsa kwenikweni. Koma ife tonse tikuyenera kumapita, mosalabadira kuti ndife ndani, tikuyenera tizipita mmodzi ndi mmodzi. Koma pali chinthu chimodzi chokha, "Tiyeni timvetsera kugamula kwa nkhani yonseyo: Wopani Mulungu ndipo sungani malamulo ake, pakuti iyi ndiyo ntchito yathunthu ya munthu," Mlaliki 12.

¹⁵ Tsopano, ine ndiribe nthawi yochuluka kwambiri ya phunziro la Sande sukulu ili, ndipo ndine wosasa mawu.

¹⁶ Mukuti, M'bale Peary Green wachita chinthu cholemekezeka. Iye anandimva ine ndikunena, usiku wathawu, "Ndinaiwala kachidutswa kanga kakang'ono ka tsitsi kondisunga ine. . ." Iye anayimba kumeneko ndipo amayesetsa kuti amupeze winawake woti awuluke nako mmalo mwanga. Ine ndinati, "Mwachedwa kwambiri, ndasasa kale mawu." Ndinayesetsa kwa zaka zambiri kuti ndipeze chondithandizira china, koma pamene ndinakapeza kameneko, iko kanachiritsa izo. Koma ine ndinakayiwala iko nthawi ino, chotero ine ndasasa mawu pang'ono. Chotero inu mupirire nane, ngati inu mungathe, mu kuyankhula.

¹⁷ Tsopano, ndi angati amakonda Sande sukulu? Oh, mai, uko nkulondola. Ndi chinthu chabwino kuwatumizako ana

anu. Ayi, ndiloleni ine ndikonze zimenezo, chinthu chabwino *kuwabweretsako* ana anu. Uko nkulondola, kuwabweretsa ana anu; inu muzibweranso nanunso. Ndi angati amadziwa momwe Sande sukulu yathu inayambira poyamba? Kodi iyo inachokera kuti? England. Kodi iyo inkatchedwa chiyani poyambirira? *Sukulu yamasanza*. Ndiko kulondola, inkatchedwa “Sukulu yamasanza.” Pamene ndayiwala dzina la munthuyo tsopano amene anayambitsa iyo. Dzina lake anali ndani? [Wina akuti, “Robert Raikes.”—Mkonzi.] Uko nkulondola, kulondola ndendende. Ndipo iye anakawachotsa ana aang’onowo pa msewu (anali amasanza, ndipo analibe malo oti apiteko, ndipo zoipa kwambiri), ndipo iye anawabweretsa iwo ndipo anayamba kuwaphunzitsa iwo Baibulo. Ndipo iyo yakula kukhala imodzi mwa ma dongosolo aakulu a mpingo, pafupifupi, lero, Sande sukulu. Ndi zabwino kumapitako. Muwonetsetse kuti muzibwera, muziwabweretsako ana anu. Ine ndikuganiza kachisi pano ali ndi aziphunzitsi, zipinda zokhala ndi zipangizo, misinkhu, ndi zina zotero. Ndipo inu otembenuka kumene amene mukubwera kumene kwa Khristu, muzitsatirabe limodzi Uthenga; muzibwera kuno ku Life Tabernacle, ndipo iwo adzakuchitirani inu ubwino.

¹⁸ Tsopano, usikuuno ife tikhala ndi mzere wa pemphero wachikale. Ife tidzangopempherera odwala momwe ife tinkachitira, M’bale Jack ndi M’bale Brown.

¹⁹ Ine ndikukumbukira ndikumuwona M’bale Brown akuyesetsa kupereka makadi apemphero amenewo, ndipo momwe iye pokhala mtumiki iyemwini, ndipo mmasiku amenewo, mu bungwe limene likanati, iwo, ankaika chiposinjolo pa iye, inu mukudziwa, “Ine—ndine m’bale wanu mu chinthu ichi,” inu mukudziwa, “inu muyenera kunditengera ine pamenepo.” Oh, iye ndithudi anali ndi nthawi yovuta, koma ankangokhala woona basi monga kuwona kungakhalire. M’bale Brown ndi mwamuna mmodzi wabwino. Ndipo chotero ife timamukonda iye.

²⁰ Ndipo pamene ine ndiwona ife tonse, atatu a ife, tikufika, tikukwawira mmwamba cha ku ukalamba, kumathero. Icho chingadzakhale chinthu cha chisoni kwambiri ngati iye sitinayike mkati mwathu chinthu chachikulu chija, chimene ife tikuchidziwa kuti ndi Choonadi. Ife tikungokonzekera kubwerera limodzi la masiku awa, kubwerera ku unyamata wathu kenanso, osadzakhalanso. . . matupi athu adzasandulika, adzapangidwa mu chifanizo Chake kuti tidzayime. “Pakuti pamene msasa uwu wa padziko lapansi wokhalamo wathu ukadzapasuka, pali wina ukudikirira kale.”

²¹ Ndipo gawo lothokoza la izo, mzanga wokondedwa, limene Ambuye Yesu wokondedwa. . . Inu amene mumandilira ine kuti ndimakuuzani Choonadi; Ambuye Yesu wokondedwa, mmawa wina pafupifupi eyiti koloko, anandilola ine kuti

ndiliwone Dziko limenelo. Tsopano, iwo sanali—sanali masomphenya; koma ine sindikufuna kuti ndinene zimenezo. Chirichonse chimene icho chinali, icho chinali chenicheni basi monga ine ndikuyankhulira kwa inu pano. Tsopano, ine ndinawona nkhope za anthu amenewo, ndipo ine sindimatha kuwazindikira iwo, iwo anali atabwerera kukhala achichepere kachiwiri. Ndipo iwo anali enieni basi ngati . . . Ine ndimakhoza kugwira manja awo ndi zinthu. Zenizeni basi monga . . .

²² Ndipo izo zinandithandiza ine, chifukwa ine ndinkakhala ndi lingaliro: munthu akafa, solo yawo yokha imachokamo. Komano pamene Iye anabwereza izo kwa ine, kuti “Ngati msomo uwu wapadziko lapansi wokhalamo wathu ukhala . . . tiri nawo kale wina.” Mukuona? Ndipo ife tikuyenera kukhala ndi chirichonse mu zitatu, kuti tipange ungwiro. Mukuona? Ndipo kuli thupi limodzi kuno, ndiye thupi limenelo apo limene liri—thupi lakumwamba, ndipo kenako thupi laulemelero mu chiukitsiro. Mwaona, izo zimapangitsa izo kukwanira. Mukuona? Chotero icho ndi . . . Si nthano, si lingaliro, si mzimu. Ndi mwamuna ndi mkazi monga inu muliri, basi ndendende.

²³ Ndipo kenako, zaka zapitazo, ine ndinakawona madera a otayika, ndipo ndinali kumeneko. Ine ndikukuza iwe, mzanga, monga munthu wachikulire, undilole ine ndikuchondelere iwe ichi, kudutsa fuko lonseli mmawa uno, usadzafune konse kukawona malo amenewo. Palibe njira iliyonse nkomwe imene ndikanatha . . . ngati ndikanakhala wojambula ndi burashi sindikanatha kujambula chithunzicho. Ngati mtumiki, sindingathe kufotokoza kwa inu. Kunena za gehena kukhala malo oyaka, ndi koipitsitsa kuchulukitsa ka milioni kuposa pamene, zowopsya zimene zimapita naye.

²⁴ Ndipo Kumwamba . . . kapena malo awa, kulikonse kumene iwo anali, ine sindikudziwa choti ndiwatchule iwo. Iye anayitcha iyo kumeneko ngati “miyoyo pansu pa guwa.” Koma pamene izo zinali, ine sindinayambepo . . . Palibe njira iliyonse yofotokoza momwe izo ziliri zazikulu. Kuli . . . Tsopano, inu mukungoyenera kungotenga mawu anga, ine ndi munthu chabe. Mukuona? Koma masomphenya awa amene nthawizonse amakwaniritsidwa monga ine ndakuwuzani inu, ndipo inu mukudziwa iwo onse akhala ali owona, *iwo* ndi owona nawonso. Chirichonse chimene inu muchita, ngati mungaphonye china chirichonse (thanzi, mphamvu, maso anu, chirichonse chimene icho chiri), musadzaphonye Chimenecho. Palibe chimene chingafanane ndi zimenezo. Ndi . . . Palibe—palibe mawu mu chinenero cha Chingerezi, amene ine ndikuwadziwa, amene angafotokoze izo. Ngati mungati “ungwiro,” ndi zodutsa pamene; “upamwamba,” izo—ndi zodutsa pamene; “zambambande,” . . . Palibe—palibe mawu amene ndikuwadziwa amene angafotokoze izo, chifukwa izo zinali . . . Ndiyeno, kuganiza, amenewo si mathero ake.

Ndinaganiza, “Ine kumachita mantha kuti ndibwere ku ichi?”

²⁵ Ine ndinati, “Kodi mumadya?”

²⁶ Anati, “Osati kuno. Sitimadya kuno, koma tikadzabwerera kudziko lapansi tidzakalandira thupi limene tizikadyeramo.”

²⁷ Chabwino, ine ndimakhoza kuwamverera iwo. Iwo anali monga *choncho*. Mukuona? Ndipo iwo. . . Ine ndinati, “Chabwino, inu muli. . .” Oh, inde, iwo ali ndi thupi. Si nthano chabe, ndi thupi. Ife timadziwana wina ndi mzake. Iwo onse anandidziwa ine, ankandikumbatira ine, mamillioni a iwo.

²⁸ Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine ndikufuna kumuwona Iye Amene wandibweretsa ine kuno.”

²⁹ Iye anati, “Iwe sungamuwone Iye tsopano, iwe ukuyenera kudikira.”

³⁰ Ine ndinati, “Nchifukwa chiyani inu munandiika ine pa. . . pamwamba apa?”

³¹ Anati, “Iwe unali mtsogoleri mmoyo.”

³² Ndipo ine ndinati, “Kodi Inu mukutanthauza kuti onsewo ndi ma Branham?”

³³ Iye anati, “Ayi! Amenewo ndi owatembenuza ako kwa Khristu.” Mukuona?

³⁴ Ine ndinayang’ana pozungulira, ndipo kenako mausiku onse ovuta, ndi mayesero, anapita, pamene ndimakhoza kuwona nkhope zawo. Mkazi wamng’ono anathamangira kumeneko, mmodzi wa akazi okongola kwambiri, ndipo iye anadzangoponyera manja ake mondikumbatira ine, ndipo anati, “M’bale Wofunika.” Ndipo pamene iye anadutsa. . . Tsopano, iye anali mkazi. Chotero. . . Koma kumeneko, sikudzakhala konse tchimo. Mwaona, zokhudzira zathu zimasinthidwa kumeneko. Iwo samadzalerako ana konse, kumeneko. Mukuona? Mwaona, zonse mofanana.

³⁵ Chimene chimapangitsa kusiyana, kugirigisha. Ndi chifukwa chake ine sindimakhulupirira za kuvina pabwalo. Palibe mwamuna. . . Ine, pamaso pa Mulungu ndi Baibulo langa, ndakhala moyo woyera, monga *choncho* mmoyo wanga pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono, monse kudutsa mu unyamata wanga. Mtsikana aliyense amene ine ndinayendapo naye, ine ndikhoza kudzayendanso kubwerera komwe ku Chiweruzo ndi iye. Mukuona? Koma palibe mwamuna, ine sindikusamala chimene iwe uli, angalole mkazi (mu kapangidwe ka mkazi) kudzikumbatira yekha pafupi ndi iwe; ngati iwe uli mwamuna weniweni wathanzi, pamakhala zogirigisha. Koma izo kunalibeko kumeneko; kulibeko zokhudzira. Nonse mumakhala azokhudzira zofanana. Mukuona? Basi chikondi choyera, chosaipitsidwa cha pa alongo ndi pa abale, kuposa momwe zingakhalire kwa wako. . . ngakhale kwa wako. . . kumukumbatira mwana wako yemwe

wamkazi wamng'ono. Mukuona? Mwana wako yemwe wamkazi, komabe iye anapangidwa... iye ndi mkazi ndipo iwe ndi mwamuna. Mwaona, izo zikhoza kupanga chinachake; koma Uko sizikanatero, tchimo lathetsedwa, zonse zathako. Mukuona? Chenicheni... Chikondi chenicheni, choyera basi.

³⁶ Ndipo ine ndinayang'ana pa mkazi ameneyo. Apo panali... ankawoneka ngati mamillioni a iwo pamenepo, ndipo iwo onse a tsitsi lalitali, ndi zovala zoyera zazitali. Ndipo—ndipo Uyu amene ankayankhula ndi ine anati, “Kodi sukumuzindikira iye?”

³⁷ Ine ndinati, “Ayi.”

³⁸ Anati, “Iye anali mu usinkhu wa zaka zake za mma nainte pamene iwe unamutsogolera iye kwa Khristu.”

³⁹ “Chisomo chodabwitsa, kumveka kwake nkokoma bwanji.” Mukuona? Palibe njira yofotokozeru konse chimene icho chiri. Mungotenga mawu anga ngati inu mukundikhulupirira ine. Muonetsetse kuti mupange... muwotchere mmbuyo mwanu mlatho uliwonse wa mdziko.

⁴⁰ Ine ndikukhulupirira mpingo ukuyamba kumvetsera Uthenga, ndipo wayamba kumvetsetsa. Koma, amzanga, mveterani, ife tikuyenera kukhala mu Kukhalapo kwa Mwana, ife tikuyenera kuti tiche. Chathu—chikhulupiriro chathu sichinakhwime. Mwaluntha ife tikumvetsera Uthenga umene Mulungu watipatsa ife, ndipo tikuwona zizindikiro zimene Iye anatiwonetsa ife, ndi kutsimikizira izo mwa Baibulo, izo ziri pamenepo, koma, oh, momwe mpingo ukuyenera kuti uzikhala mu Kukhalapo Kwake kufikira iwo utacha, inu mukudziwa, ndipo kumakoma mu Mzimu kuti iwo ukhoze kusamba mpaka pansu. Nthawizina poyankhula Uthengawu, umakhala waukali, umayenera kuwuswa iwo monga choncho, chifukwa umayenera kukhomerera msomali kuti iwo ugwire. Koma pamene Mpingo ukadzangomvetsetsa kamodzi Izo, Osankhidwa akadzaitanidwa atuluke ndipo adzalekanitsidwa, kenako adzakakhala mu Kukhalapo kwa Mulungu, ine ndikudziwa kuti chidzakhala chinachake monga anthu anali Kumeneko pamene Iwo uzidzanyamuka Mkwatulo Wake.

⁴¹ Ine ndimati ndiyankhule mmawa uno pa *Mkwatulo*, koma ndiribe mawu okwanira ochitira zimenezo, ndipo chotero inu mungopirira nane ine kwa kanthawi pang'ono, pamene ndikufuna kuti ndiyankhule pa phunziro la: *Malo Okhawo Oprekedwa Ndi Mulungu Opembedzerapo*.

⁴² Tsopano, ndi mutu wopambana waukulu. Chotero tiyeni tipemphere tsopano. Ndipo uko kudutsa maiko mmawa uno, kulikonse kumene inu muli, weramitsani mitu yanu mphindi pang'ono chabe. Mukhale owonamtima kwenikweni tsopano, ife tikuyandikira Mawu a Mulungu, amene ali Mulungu mu mawonekedwe a chilembo.

⁴³ Mlembi wamkulu wa Bukhu ili, “Ilo ndi Mbewu,” ife timaphunzitsidwa, “kuti wofesa anafesa,” anatero Mlembiyo. Tsopano, ife tikuzindikira kuti mbewu imamera ngati ili mu nthaka yoyenera. Chotero, Atate, kodi Inu mmawa uno mungachotse mitungwi ndi nthula, ndi kusakhulupirira, ndi maganizo okaikira kuchokera mmitima yathu; kuti Mawu a Mulungu athe kukula momasuka, kuthiriridwa ndi Mzimu mmitima yathu, kuti ife tithe kukhala anthu a Mulungu. Perekani izi, Atate. Ndiyo mitima yathu. Osati kwa ife tokha amene tazindikira izi, koma pakhale ena mdziko lonse, mtima wa aliyense ukuyaka ndi chikondi ndi chifundo, upite kukayesera kumupindula m’bale wotayikayo, mlongo wotayikayo. Perekani izi lero, Mulungu. Ife tikuyang’ana kwathunthu kwa Inu, pakuti Inu ndinu Namulondola wathu ndi Ambuye wathu. Chotero ife tikupemphera kuti Inu mutilondolere ife mu Mawu Anu lero, ndi kutipatsa ife madalitso Anu. Kudzera mu chisomo Chanu ndi mu Dzina Lanu ife tikupempha izi. Amen.

⁴⁴ Tsopano, tiyeni titenge kwa mutu wathu. . . Ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu Bukhu la Deuteronome, Chipangano Chakale, mwa kungoyika kwa Lemba. Ine ndiri ndi zolemba zingapo zimene ndinazilemba mwamsanga nditabwera kuchokera ku kadzutsa ndi M’bale Vayle.

⁴⁵ Sindinakwanitse kumuthokoza bamboyo uko ku hotelo kuja. . . malo odyera aja usiku wina, amene anatiripirira wathu—mgonero wathu. Mkazanga ndi ine ndi mtsikana wanga wamng’ono tinali kumeneko, ndipo pamene ine ndinapita kuti ndikalipire bilu yanga, winawake anali atailipira iyo. Aliyense amene anateroyo, ine ndikukuthokozani inu. Anati, “Munthu amene anakhala kumapeto kwa mpando.” Ndithudi panali gulu lonse mmenemo limene ife timalidziwa. Tsopano, ine. . . mtundu wina wa Kickapoo, chinachake chonga icho, malo kunja kuno, kumalo odyera kumene ife tinali. Zikomo inu, aliyense amene anachita zimenezo. Aliyense wa inu, Mulungu akudalitseni inu.

⁴⁶ Tsopano, mu mutu wa 16 wa Deuteronome, ndi kusunga kwa pasaka. Chotero ife tikufuna kuti tiwerenge pafupifupi ndime zoyambirira pang’ono, zoyambirira zinai kapena zisanu, ndime zisanu ndi imodzi apa.

Muzisunga mwezi wa Abibu, ndi kusunga pasaka. . . (Zimenezo zikutanthauza “Epulo.”) . . . YEHOVA Mulungu wanu: pakuti mmwezi uwu wa Abibu YEHOVA Mulungu wanu anakutulutsani mu Igupto usiku.

Inu muzipereka nsembe ya pasaka kwa YEHOVA Mulungu wanu, ya zoweta ndi ng’ombe pamalo amene YEHOVA adzasankhe kuyikapo dzina lake. . .

Inu muzidya mkate wopanda chotupitsa mmenemo; masiku seveni inu muzidya mkate, wopanda

chotupitsa—mkate umene, . . . inu munaturuka mdziko la Igupto mwaliwiro: . . . inu muzikumbukira—tsiku limene inu munaturuka mdziko la Igupto masiku onse a moyo wanu.

Ndipo sipadzakhala . . . mkate wopanda chotupitsa udzawoneke ndi inu mmalire anu onse masiku seveni; komanso sipadzakhala chirichonse cha mnofu, chimene inu mwapereka nsembe tsiku loyamba madzulo, khalani usiku wonse kufikira mmawa.

Inu musamapereke nsembe pasaka mkati mwa zipata, zimene YEHOVA Mulungu wanu wakupatsani inu:

Koma pamalo amene YEHOVA Mulungu wanu anasankha kuti adzayikepo dzina lake, pamenepo inu muzipereka msembe ya pasaka madzulo, pa kulowa kwa dzuwa, pa nyengo imene inu munatuluka ku Igupto.

Tsopano Ambuye awonjezere madalitso Ake ku kuwerenga kwa Mawu Ake.

⁴⁷ Tsopano, kodi maikrofoni ali ndi mazenene mwa iwo? Usiku wathawu ndinamva kuti anali nawo. Kodi inu mukundimva bwino bwino, paliponsepo? Simukundimva. [M'bale Branham akukonza maikrofoni—Mkonzi]. Alibwino pamenepo? Apa bwanji alibwino, kuyankhula ndi maikrofoni mowayandikira monga chonchi? Ine ndangosasa mawu pang'ono, chotero ine ndikuyima mowayandikira mmawa uno pa chifukwa chimenecho, ndipo ine ndikuyembekeza kuti M'bale Peary akhoza—akhoza kuzitengera izo kunja uko. Kodi mukumva izo zonse bwino bwino tsopano? Ndikuganiza kuti akonza izo. Chabwino.

⁴⁸ Tsopano, a . . . Chinthu chimene ine ndikufuna kuti ndiyankhule mmawa uno ndi chakuti Mulungu ali ndi malo amodzi okha amene wopembedza angakumane naye Mulungu, malo amodzi okha. Kudutsa mmibadwo ambiri akhala akufunafuna malo obisika awa a Mulungu, kudutsa mmibadwo yonse. Ngakhale Yobu ankafuna atadziwa kumene Iye ankakhala, “Ngati ine ndingakhoze kokha kupita ku nyumba Yake ndi kukagoda pa chitseko Chake.” Yobu ankafuna kupeza malo okhalapo a Mulungu, chifukwa kumeneko Mulungu ndi banja Lake amapembedzedwa pamodzi.

⁴⁹ Monga dzulo, mu uthenga dzulo mmawa, ife tikupeza kuti pali kuthekera kwakuti munthu akhoza kumamupembedza Mulungu pachabe, ndi kupembedza moonamtima. Mulungu anatikonzeratu ife zinthu zonsezi, koma nkhani yake ndi yakuti, timayenera kufufuza kuti tipeze pamene izo ziri. Paulo anamuuza Timoteyo kuti afufuze, ndi ku—kuti azikhala mu nyengo ndi kunja kwa nyengo, azikhala wokonzeka kupereka a—mawu kapena . . . a chiyembekezo chimene chinali mwa iye.

⁵⁰ Tsopano, zinthu zonsezi ziri mmenemo. Ndipo ife tikupeza...Nthawizina ine ndikanakonda nditabwera ku Shreveport kumene ife tingangokhala ndi pafupifupi masabata awiri kapena atatu kuti tidzangotenga maminiti sarte usiku ndipo basi pa kuphunzitsa, mwaona, basi kudzangokhala mu Mawu, ndime zobisika izi, mwaona, pamene tingapezere momwe tingaloweremo. Ndipo iwe nkumangoyang'ana, kumangotsatira chitsogozo cha Mulungu, pamakhala fungulo limodzi lokha kwa khomo lililonse. Izo nzoona. Ndipo palibe fungulo lina, ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe ilo likuwonekera ngati ndi limenelo, Mulungu samakhala ndi fungulo la chigoba; amangokhala ndi fungulo limodzi. Ndipo tsopano, inu mukuyenera kukhala ndi fungulo limenelo, kapena chitsekocho sichitseguka. Ziribe kanthu ndinu owonamtima bwanji, simungatsegulebe chitsekocho.

⁵¹ Tsopano, ndi angati anali pa kadzutsa wa dzulo, mmawa wina? Chabwino, ine ndikuganiza ambiri, pafupifupi nainte percenti a inu, kapena kupitirira. Kuti ndiyikire maziko izi, chimene nditi ndinene, Davide anadzozedwa kukhala mfumu (anadzozedwa ndi Mulungu), mfumu yaikulu kwambiri imene Israeli anayamba wakhalapo nayo, kunja kwa Ambuye Yesu (amene ali Mulungu) Wodzozedwa Uyo. Davide ndi mwana Wake, kapena, Yesu anali Mwana wa Davide molingana ndi mabadwidwe, mthupi. Ndipo Iye ndi woti adzakhala pa mpando wachifumu wa Davide monga cholowa chimodzi, monga—kalonga nthawizonse amalandira cholowa mpa—mpando wachifumu wa mfumu.

⁵² Zindikirani, tsopano, kuti Davide pokhala wodzozedwa, komabe ndi kudzoza kumene iye anachita, iye anatulukuka mu chifuniro cha Ambuye ndi kudzoza kumeneko; ndipo anthu onse, osatenga kuyendetsa kwa Lemba kapena fungulo la vumbulutso ili, onse a iwo odzozedwa nawonso, iwo onse, pamodzi, akufuula ndi kutamanda Mulungu pa chinthu chimene chinkawoneka cholondola ndendende: kuti awabweretsenso Mawu a Mulungu ku nyumba ya Mulungu. Koma Davide anali mfumu osati mneneri. Mukuona? Iye...Munali mneneri mu dziko woti azichita naye izo, ndipo Mulungu sanalemekeze zochitika zonsezo chifukwa iwo sanagwiritse ntchito fungulo loyenera. Chitsekocho sichinatseguke. Ndipo tsopano ife tikuyenera kukumbukira zimenezo, ndi kuzisunga izo mmalingaliro. Pamakhala...Chirichonse cha Mulungu, njira imodzi inayake iyenera kuti zizichitikira, ndipo izo zimakhazikitsa izo. Tsopano, apo Mulungu ali ndi Mpingo winawake umene Iye amakumanamo ndi anthu, ndipo Iye adzakulandirani inu mu Mpingo umenewo osati mpingo wina.

⁵³ Ine ndikunena izi chifukwa nthawi zambiri ndakhala ndisakumvetsetsedwa, ndipo anthu andiwuzapo ine . . .

Ine ndikuti, “Kodi inu ndinu Mkhristu?”

“Ndine wa Baptisti.”

“Kodi ndinu Mkhristu?”

“Ndine wa Methodisti.”

“Kodi ndinu Mkhristu?”

“Ndine wa Pentekoste.”

⁵⁴ Tsopano, mwaona, zimenezo sizimatanthauza chinthu chimodzi kwa Mulungu. Inu mukungowunguza ndi fungulo lolakwika. Koma liripo fungulo lolondola, liripo limodzi kumene Mulungu. . . Mulungu sanalonjeze kuti adzakumana nanu inu ngati wa Methodisti, kapena wa Baptisti, kapena wa Chipentekoste, kapena osati chipembedzo china. Iye samaziganizira nkomwe zipembedzo, izo zimatsutsana ndi Iye.

⁵⁵ Pa Uthenga wautali umenewo, ine ndidzawutenga Iwo ku kachisi posakhalitsapa. Ndipo ndikadzatero M'bale Jack adzaumva Iwo, ndiyeno inu mudzawona chimene inu mungadzafune kuti muchite nawo Iwo, chifukwa Iwo udzajambulidwa.

⁵⁶ Tsopano, anthu amachita ngati kuti Mulungu ndi wokakamizika kungokumana nawo pa maziko a fioloje yawo. Tsopano, anthu amachita monga choncho. Iwo samayanjana ngakhale wina ndi mzake. Utatu wa Pentekosite samayanjana ndi Umodzi, ngakhale a Umodzi samayanjana ndi a Utatu. Amethodisti sangatero ndi Abaptisti, chifukwa wina ndi wachilamulo ndipo wina ndi wa Calvinisti, chotero iwo alibe chiyanjano nkomwe. Ndipo iwo amawasokoneza malingaliro a anthu moyipa kwambiri mpaka amatsutsana wina ndi mzake.

⁵⁷ Ine ndinapita kukapemphera, nthawi ina kale, mchipinda cha chipatala. Uko kunali dona atagona pamenepo akudwala kwambiri, akupita ku opareshoni, iwo anka yembekezera kuti iye afa. Dona wina atagona pamenepo (ine ndinaitanidwa kuti ndimupempherere iye.), ine ndinati kwa iye, “Kodi mungasamale mphindi chabe ngati ine ndingapemphere?”

⁵⁸ Ndipo iye anati, “Kokani katani limenelo!”

⁵⁹ Ndipo ine ndinati, “Ine ndikupepesa.” Ine ndinati, “Ine ndimangoti ndipemphe pemphero.”

⁶⁰ Iye anati, “Kokani katani limenelo!”

⁶¹ Ine ndinati, “Inde, amayi.” Iye ndi mwana wake wamwamuna atakhala pamenepo, mawonekedwe achizolowezi a *Ricky*. Ndipo ine ndinati, “Chabwino, kodi inu si Mkhristu?”

⁶² Iye anati, “Ndife a Methodisti!”

⁶³ Ndinati, “Chabwino, ine sindinakufunseni inu zimenezo, ine ndakufunsani inu ngati inu muli ‘Mkhristu.’” Mukuona?

⁶⁴ Ndipo chotero iye anati, “Kokani katanilo!”

⁶⁵ Mwaona, chifukwa winawake amene sanali wa Methodisti amafuna kuti amupempherere mkazi amene amafa, chimene iye anali nayenso. Koma chifukwa izo sizimagwirizana mu bungwe lake lomwe, iye sankafuna konse kuti azimve izo kapena kukhala ndi kanthu kochita ndi izo. Ngati ameneyo si Mfarisi, ine sindinamuwonepo mmodzi!

⁶⁶ Dikirani mpaka mudzamvere *Mkukuluzi Wa Serpenti*. Huh. Chabwino. Tsopano, taganizani tsopano kuti chipembedzo chawo ndi chokhacho chimene chimalembetsa kwa Mulungu: “Mulungu sangakumveni inu pokhapokha ngati muli wa Methodisti, kapena wa Baptisti, kapena wa—wa Utatu, kapena Umodzi,” kapena chinachake chonga chimenecho. Uko nkulakwitsa!

⁶⁷ Ndipo ndicho cholinga changa; koma ngati pali—khumbo mmalingaliro a anthu ndi mmitima yofuna kuchita bwino. . . Ine sindikukhulupirira kuti mkaziyo amachita zimenezo chifukwa. . . kapena wina aliyenseyo. Wa Methodisti sangadzuke ndi kutengera mpingo wa Methodisti chifukwa iye—amadziwa kuti ndi zolakwika. Mwamunayo amaganiza kuti ndi zolondola. Ine sindikukhulupirira kuti wa Utatu angamutsutse wa Umodzi, kapena wa Umodzi, wa Utatu, mu Pentekoste, chifukwa akufuna kuti akhale wosiyana, iye amaganiza kuti akulondola, ndipo inu mukuyenera kulemekeza malingaliro akewo. Inu mukudziwa, bulangete limatambasukira mbali ziwiri zonse. Koma, kumbukirani, mu zonsezo, ngati muli chinachake mu mtima wa mwamuna kapena mu mtima wa mkazi kuti iwo anakhulupirira kuti izo ndi “zolondola,” ndiye pakuyenera kukhala penapake pamene pali polondola. Monga ndimanenera nthawi zambiri, “Pamene chakuya chikuitanira ku chakuya, pamayenera kukhala chakuya choti chiyankhire kuyitana kumeneko.”

⁶⁸ Inu mukudziwa, ife tinauzidwapo kuti—kuti nthawi ina galu wam’madzi anayendapo mmphepete mwa—mwa nyanja, ndi miyendo. Koma tsopano iye alibe miyendo, iyo inasanduka mapiko chifukwa iye ankatha. . . ankasowekera mapikowo pamene iye anaichotsa iyo kumtunda, nyama ya ubweya, kupita nayo ku nyanja; chirengedwe chinamupangira iye mapiko mmalo mwa miyendo, chifukwa iye ankatha kusambira kuposa momwe iye ankachitira ndi kuyenda kwake.

⁶⁹ Ine sindingakhoze kuganiza za munthu wamkulu uyu tsopano amene anapita ku South Pole. Dzina lake anali ndani? Byrd. Iwo amanena kuti iye anapanga zikhotho za ng’ombe zina, pa kufotokoza uku; kuti anatenga ng’ombe kuti azikamwa mkaka. Ndipo ankapanga zikhotho za ubweya kuti ng’ombezo zisafe ndi kuzizira. Koma pamene anakafika kumeneko, iwo sanasowe chikhotho cha ubweya chirichonse, chirengedwe chinali chitaumeretsa iwo kamodzi. Mukuona? Bwanji? Pasanakhale chipsyepsye pa nsana pa nsomba,

pankayenera kukhala madzi oti iyo izisambiramamo kapena iyo sikanakhala ndi chipsyepsye. Apo...Pasanakhale mtengo woti umere *mu* nthaka, pankayenera kukhala nthaka poyamba kuti iwo ukuliremo, kapena apo sipakanakhala mtengo.

⁷⁰ Chotero, inu mwaona, bola ngati pali chinachake mu mtima wa munthu chikuyitanira chinachake, pakuyenera kukhala chinachake kunja uko choti chiyankhire, kuti chikhutitse kuyitana kumeneko.

⁷¹ Mkazi...Kupimidwa kwa mtembo kunachitika kuno kanthawi kapitako pa mkazi amene anafa. Ndipo chifukwa, iwo—iwo amati, chimene chinamupha iye, iye amadya anyezi mowirikiza basi, nthawi zonse. Ngati iye akanati samadya anyezi, mutu wake bwenzi ukuyabwa, ndi chirichonse; iwo samakhoza kuzimvetsa zimenezo. Chotero atagwira zofufuzazo, iwo anapeza chotupa mwa mkaziyo cha mtundu wina wa timakhungu; iwo anali ndi—dzina la izo. Ndipo iwo amakhoza kutenga chophukacho ndi kuchiyika icho m'mbale ya anyezi, ndipo icho chinkamusungunula anyezi yenseyo usiku wonse. Mukuona? Icho chinali chiyani? Chinali chinachake mwa mkaziyo chikuitanira anyezi, ndipo ngati pakanakhala kuti palibe anyezi sipakanakhala chophukacho.

⁷² Mwakuyankhula kwina, pakuyenera kukhala Mlengi choyamba, pasanakhale chirengedwe. Mukuona?

⁷³ Tsopano, ngati mu mtima wa munthu muli chokhumba... Monga Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, kwa Akatolika, ena onsewa, akuyesera kuti apeze njira imodzi yoona imeneyo, ndipo iwo amauzidwa ndi ansembe awo ndi azibusa, ndi ena otero, kuti, “Iyi ndi njira yoona.” Iwo amati, wansembe amati, “Palibepo chipulumutso kunja kwa mpingo wa Katolika.”

⁷⁴ Chabwino, mpingo uliwonse umatenga ake... malingaliro awo omwe. Ena a iwo sangavomereze, koma iwo amazichita izo ndi zochita zawo. Zochita zanu zimayankhula mokweza kuposa mawu anu. Izo ndi basi...Mwanjira ina, iwo ndi achinyengo kwambiri kuposa momwe Akatolika aliri. Akatolika amavomereza izi momveka, “Ndikukhulupirira kuti ichi ndi chinthu chokhacho,” koma iwo sangachite izo. Iwo amabisa izo, koma zochita zawo zimatsimikizira chimene iwo akuganiza. Mukuona?

⁷⁵ Tsopano, pakuyenera kukhala ndiye malo amodzi, chifukwa mumakhala chikhumbo mu mtima wa munthu kuti awapeze Iwo. Ndipo ine ndikuganiza kuti Mawu a Mulungu ali ndi yankho la chirichonse chimene ife tikuchisowa. Chotero Mulungu ali ndi yankho, ndipo tiyeni tifufuze ilo tsopano mu Malemba. Ndiyeno ngati Mulungu angatiwonetse ife mwa Malemba malo okhawo, malo okhawo (chipembedzo chokhacho, ngati ziri chomwecho), njira yokhayo imene Mulungu adzakumane ndi munthu, ndiye

ife tikuyenera kugwiritsitsa kwa icho chifukwa ife tachipeza Choonadi cha Baibulo, chimene Ilo limanena.

⁷⁶ Tsopano, mawu akuti *Deuteronome*, mawuwo pawokha amatanthauza “malamulo awiri,” mawu akuti *Deuteronome*. Ndipo Mulungu ali ndi malamulo awiri. Malamulo awiriwo: limodzi la iwo ndi kusamvera ku Mawu, ndi kufa; ndipo linalo ndi kumvera ku Mawu, ndi kukhala moyo. Ndiwo malamulo awiri, ndipo *Deuteronome* amatanthauza malamulo awiri amenewo. Iwo onsewo awonetseredwa mwamtheradi kwa ife mu Lemba. Limodzi la iwo ndi imfa, linalo ndi Moyo; Moyo ndi imfa. Mulungu amachita kokha mu Moyo, Satana mu imfa yokha. Ndipo izi zinawonetseredwa ku dziko lapansi poyera, mowonekera pamaso pa diso lirilonse, ndipo palibe chowiringula kwa ife. Limodzi la iwo linawonetseredwa pa Phiri la Sinai pamene lamulolo linaperekedwa, limene linaweruzira mtundu wonse wa anthu ku imfa; linalo linaperekedwa pa Phiri la Kalvare, limene linabweretsera mtundu wonse wa anthu ku Moyo, pamene chilango chinalipiridwa mwa Yesu Khristu. Malamulo awiriwo a *Deuteronome* anakwaniritsidwa mu zinthu ziwiri, zazikulu izi.

⁷⁷ Ine ndikufuna inu muzindikire kachiwiri, panalinso mapangano awiri omwe anaperekedwa. Pangano limodzi linaperekedwa kwa Adamu, limene linali pa mangawa, monga lamulo: “*Ngati* simudzakhudza ichi, ndiye mudzakhala ndi moyo; koma *ngati* mudzakhudza ichi, inu mudzafa.” Limenelo linali lamulo. Kenako panali lamulo lina linaperekedwa kwa Abrahamu, limene linali mwa chisomo, mopanda mangawa: “Ine ndakupulumutsa iwe ndi mbewu yako yapambuyo pako.” Ameni! Icho ndi choimira cha Kalvare, osati choimira cha—cha—cha pangano la Adamu, ndi pangano la Abrahamu.

⁷⁸ Koma tsopano tikumumva Iye akunena kuti pali malo amodzi okha amene Iye angakumane ndi munthu kuti apembedze. Ife taziwerenga izo pomwe apa mu phunziroli. Ife tilozera kwa izo, mmbuyo, mu maminiti pang’ono.

⁷⁹ Ndiye ngati alipo malo amodzi okha amene Mulungu amakumana ndi munthu, kulibwino tizikhala osamala kwambiri. Tsopano tiyeni tiyike pambali miyambo yathu mmawa uno, ndipo...mu phunziro la Sande sukulu ili, ndipo tikhale otsimikiza kwambiri kuti ife tawapeza malo amodzi amenewo. Chifukwa, Mulungu wanena apa, Iye sadzakulandirani inu kwina kulikonse. Mpingo wina uliwonse, Iye sadzakulandirani inu. Mu Mpingo Wake wokha, ndi malo okhawa amene Iye angakulandireni inu.

⁸⁰ Tsopano, “Inu mukuti chiyani, M’bale Branham? Ngati ndiri wona mtima?” Ayi.

⁸¹ Kumbukirani, Yesu ankayankhula ndi anthu ena owona mtima, opembedza a tsiku Lake, ndipo Iye anati,

“Pachabe inu mundipembedza Ine.” Zolondola, kupembedza koono kukuchokera pansi pa mitima yawo. “Pachabe inu mumandipembedza Ine, mumaphunzitsa chiphunzitso malamulo a anthu,” kapena kachikhulupiro kawo ka chipembedzo. Moonamtima, molemekeza, mwachipembedzo basi monga momwe iwo angakhali. Ndipo izo sizinali zatsopano kwa Afarisi. Kaini ndi Abele, opembedza awiri oyambirira amene anabadwa, kubadwa kwachirengedwe kuno pa dziko lapansi, mwamtheradi kunadza mu khalidwe lomwelo.

⁸² Kaini anali wachipembedzo basi monga Abele. Awiri onsewo anamanga maguwa. Awiri onsewo ankamukonda Mulungu. Awiri onsewo ankapereka nsembe. Awiri onsewo ankapembedza. Awiri onsewo ankapereka chakhumi. Awiri onsewo ankachita chirichonse mofanana basi. Koma Abele, mwa *chikhulupiro* chimene chiri “vumbulutso,” Mawu a Mulungu anaululidwa, anayikidwa poyera, anawonetsera, ndi kutsimikizira. Ulemelero! Kaini ankapereka nsembe, koma Mulungu sanaitsimikizire iyo. Mulungu ankafuna kupembedzedwa, ndipo Kaini anapereka nsembe, koma Mulungu sanaitsimikizire iyo. Koma mwa mpita woona. . .

⁸³ Inu mukuti, “Chabwino, mpingo wanga ndi Iwo. Wanga. . .”

⁸⁴ Dikirani miniti yokha. Mulungu amatanthauzira Mawu Ake Omwe mwa mfundo Zake zimene Iye anayankhuliramo. Mwaona, Kaini anati, “Ndine wachipembedzo. Ndine wokonda Mpangi wanga. Ine ndikupereka kwa Inu guwa labwino ili. Ine ndikupereka kwa Inu nsembe iyi. Ine ndinamanga zinthu zonse izi, Ambuye, chifukwa ine ndimakukondani Inu.” Abele ananena chinthu chomwecho. Tsopano, ndi amene wavomeredwa, amene watsimikiziridwa. Ndipo Mulungu anadzatsika pansi ndipo anadzalandira nsembe ya Abele, chifukwa mwa vumbulutso iye anakhudza mpita woona wa Mulungu umene unalandiridwa.

⁸⁵ Tsopano penyani mzimu wa Kaini umenewo ukubwera kudutsa mu Lembu, mpaka ku tsiku lotsiriza lomwe lino. Wachikhazikitso? Wachikhazikitso basi monga momwe winawo unali.

⁸⁶ Tayang’anani pa mneneri Balamu ndi mneneri Mose. Awiri onsewo anali ndi maguwa seveni, maguwa a Yehova, magazi pa lirilonse; ndipo osati zokhazo, komanso nkhoa zamphongo pa lirilonse. Mu chiwerengero, nambala yolondola ndendende, *seveni*, “mwangwiro,” nkhoa seveni. Ndendende mofanana basi, maguwa onsewo. Mwachikhazikitso monga winayo anakhalira, winayonso anali. Koma kodi Mulungu anamtsimikizira ndani? Mukuona? Mukuona? Iye amene anali mu Mawu Ake. Chikhazikitso sichitanthauza zambiri; ndi vumbulutso la Mulungu.

⁸⁷ Tsopano taganizani! Amuna awa, chifukwa chimene iwo anaitanidwa ndipo anayikidwa mu chikhalidwe ichi (Afarisi awa) ndi Yesu, anati, “Pachabe inu mumandipembedza Ine”? Kumupembedza Iye: kupembedza kwenikweni, kupembedza kowona kochokera mmitima mwawo. “Inu... Pachabe inu mumandipembedza Ine.” Bwanji? Mumaphunzitsa chiphunzitso mwambo wawo wa anthu. “Poteru mumapangitsa malamulo a Mulungu kukhala opanda ntchito kwa anthu.”

⁸⁸ Ngati ine ndikanakuphunzitsani inu uthenga wa Methodisti, izo sizikanagwira ntchito pa inu, ino ndi nthawi ya Mkwatibwi. Ngati Mose akanaphunzitsa uthenga wa Nowa, sukanagwira ntchito. Ngati Yesu akanaphunzitsa uthenga wa Mose, sukanagwira ntchito. Chifukwa mbewu yokonzedweratu ili pamenepo imeneyo idzathiriridwa kokha ndi mtundu umenewo wa madzi amene anaperekedwera ku mbewu imeneyo. Mukuona? Siidzakula mu zikhalidwe zina zirizonse. Ziyenera kukhala zikhalidwe zimene zimakulitsa iyo.

⁸⁹ Tsopano, inu mukhoza kutenga dzira la nkukhuku ndi kuliya ilo mu chofungatira, limene likuyenera kukhala pansa pa nkukhuku, koma ilo lidzaswa mulimonse. Liyikeni ilo pansa pa mwana wa galu ilo liswa. Ndi kutenthako, chikhalidwe chimene chimapangitsa ilo kuti liswe. Chotero ilo likuyenera kukhala pansa pa chikhalidwecho. Inu mukhoza kutenga dzira labwino lamoyo ndi kudzaliyika ilo pansa pa nkukhuku yakufa, ilo silidzaswa. Mukuona? Mwaona, ndi chikhalidwecho.

⁹⁰ Chabwino, umo ndi momwe zikukhalira mu m’badwo uno umene ife tikukhalamo, inu mukuyenera kupeza chimene njira ya Mulungu ili yochitira izo ku m’badwo uno. Ndicho chimene Martin Luther anachipeza, ndicho chimene John Wesley anachipeza, ndicho chimene Achipentekoste anachipeza mu m’badwo wawo. M’badwo wa Mulungu ndi nthawi yoti achitire izo.

⁹¹ Tsopano, Achipentekoste. M’bale ameneyo, mmodzi... ine ndikukhulupirira ake... limodzi la maso ake linali litachotsedwa, m’bale wachikuda amene anayambitsadi uthenga wa Chipentekoste mu California, Azusa Street yakale. Iye anasekedwa, chifukwa iye anali wachikuda. Iye anaserewulidwa, koma iye anabweretsa uthenga wa m’badwo umenewo. Wathupi laling’ono chabe, munthuyo sankatha kulemba dzina lake lomwe, koma Ambuye anali ataulula kwa iye kuti uwu unali m’badwo wa kubwezeretsa kwa mphatso zimenezo, ndipo izo zinabwera. Ziribe kanthu *chimene* chinanenedwa, izo zinabwera. Koma aliyense analowa mu chikhalidwe cha izo, ndipo anawona kuti unali m’badwo umenewo, ndipo anamuwona Mulungu akutsimikizira kuti anthu amenewo amatha kuyankhula mmalirime, ndi zina zotero, izo zinachitika. Komano pamene iye anapita ndi kukakhomerera izo pansa kuti “uwu ndi umboni wokhawo,” izo

zinapha izo. Mukuona? Zikupitirirabe, mwaona. Izo zinachita izo. Ndiye iwo anayamba kulekanitsa *ichi, icho*, ndi kupanga zipembedzo; ndipo wina akubwera pa mtambo, ndipo winayo akubwera mu thengo. Ndipo oh, mai, apo izo zikupita.

⁹² Izo ndi zimene zipembedzo zimachita. Mukuona? Mulungu si woyambitsa chipembedzo, chifukwa chipembedzo ndi Babeloni, ndipo Iye si woyambitsa chisokonezo. Ife timamuwona iye yense. . . Sumasowekera nkomwe kuti uchite kukhala waluntha kuti uziwone zimenezo. Ndi Babeloni! Mukuona? Mwambo (taganizani za zimenezo), anthu owonamtima. Tsopano, komabe, chifukwa iwo amakhulupirira izo, pakuyenera kukhala malo amodzi owonamtima amene Mulungu amakumana.

⁹³ Tsopano zindikirani ndime 2. “Kapembedzeni pamalo amene *Ine* ndawasankha.” Nsembe, ndithudi, kumene iwo ankapembedza pa nsembeyo. “Malo amene *Ine* ndinawasankha; osati amene inu munawasankha, amene munthu anawasankha. Koma amene *Ine* ndawasankha, muzipembedza pamalo amenewa.” Zikuwonetsa kuti pali malo amodzi okha, enawo ndi pachabe. Iwo sakuyenera kukhala a kusankha *kwanu*, koma akuyenera kukhala akusankha Kwake.

⁹⁴ “Chabwino, sindikuyenera kupita ku tchalitchi.” Kapena, “Ndinu a maganizo operewera! Bwanji, inu mumakangana ndi akazi za kulalikirira, ndi. . . kapena akazi za kudula tsitsi lawo, ndi amuna za zinthu zina izi. Bwanji, ndinu amalingaliro operewera!”

⁹⁵ Chabwino, inu simukusowa kuti mutenge njira ya Mulungu pa izo, inu musingopita uko kumene iwo amachita zimenezo. Mukuona? Ndipo inu mudzapeza kuti izo ziri mu Lemba, chotero, “Pachabe iwo amandipembedza *Ine*.” Yesu an kayankhula za chinthu chomwecho. Mukuona?

⁹⁶ Kutu kadontho kakang’ono kalikonse, chirichonse, inu mukuyenera kukhala okhulupirika. Nthawizonse umakhala waung’ono—mpesa waung’ono, wamng’ono—nkhandwe yaing’ono imene imawononga mpesa. Nthawizina umachoka. . . Sizinthu zikuluzikulu zimene umachita, ndi zazing’ono zimene umazisiya osazichita. Kumbukirani, unyolo umakhala wamphamvu kwambiri pa malo ake ofooka olumikizira. “Odala ndi iwo amene amachita malamulo *onse* a Mulungu, kuti akakhale nawo ufulu wolowamo.” Kuchita *zonse* zimene Mulungu ananena.

⁹⁷ Ngati Ilo linanena kuti akazi azikhala ndi tsitsi lalitali, inu mukuti. . . munthu anandiuza ine osati kale, anati, “Ine sindimalalikira chipembedzo cha chingwe cha zovala.”

⁹⁸ Ine ndinati, “Ndiye iwe sukulalikira Uthenga.” Eya.

⁹⁹ Mulungu anaziyika izo pamenepo, Iye ananena zoti tizichita. Ndipo inu mwina muchita izo. . . Ndicho chinthu chanu chachirengedwe, chomveka bwino. Chinthu chaching’ono

bwanji. . . chiyani. . . chaching'ono chosafunikira. Yesu anati, "Odala ndi iwo amene angatenge zinthu zazing'ono zonse, nkumachita zinthu zazing'onozo." Ndipo mkazi kulisiya tsitsi lake kuti likule, ndizo basi. . . bwanji, ndi chinachake basi chimene *iyе* angachite, ndipo iye sangachite nkomwe izo. Iye sangachite nkomwe izo.

¹⁰⁰ "Oh, tiphunzitseni ife zinthu zazikulu."

¹⁰¹ Kodi ungaphunzitse bwanji zinthu zazikulu, pamene mukulephera kuchita zophwekazo, chinthu chawamba? Chifukwa, inu mwaona, cholinga chanu ndi chofuna chanu ndi zolakwika.

¹⁰² Ndi chikondi chanu kwa Mulungu, "Ambuye, ine sindikusamala zimene Inu mukufuna kuti ine ndichite, ndine wololera kuchita zimenezo." Zikamatero inu mukufika penapake, koma ngati inu simukuchita zimenezo mwanjira imeneyo, momwe Iye ananenera kuti muzichitira izo. . .

¹⁰³ Ndi kusankha Kwake, "Malo amene Ine ndawasankha." Ndiko kumene mumapembedzako ndi nsembe yanu.

¹⁰⁴ Inu mumayika. . . Kaini ankabweretsa nsembe yake, Abele ankabweretsa yake, zimatengera malo amene inu mukuitengerako iyo. Ngati inu mukuitengera iyo mu malo amene Iye wawasankha, izo zidzakhala bwino bwino, Iye adzailandira iyo; ngati sichoncho, Iye sadzailandira iyo. Sindikusamala, ndi nsembe yomweyo, chirichonse chimene icho chiri, iyo ikanali a- . . . yokanidwa, pokhapokha iyo itabweretsedwa ku malo ena ake.

¹⁰⁵ Tsopano ife tikufuna kuti tifufuze pamene ife tikufuna kubweretsa nsembe iyi. Ife tikhoza kufufuza. . . Ife tonse tikufuna kupita Kumwamba. Sichoncho ife? Ndipo ife tonse tikudziwa kuti tachita zolakwika. Ife tonse timakhulupirira kuti Yesu ndi Nsembe. Tsopano ife tikufuna kuti tidziwe kumene tingamutengere Iye, iyo—iyo idzalandiridwa. Mukuona? Uko nkulondola. Baibulo limatiuza ife kumene tingaitengere iyo, mwaona, ndipo iyo idzalandiridwa; kunja kwa kumeneko, iyo siidzalandiridwa.

¹⁰⁶ Tiyeni tizindikire apa malo amene Iye anawasankha kuti nsembe iyikidwepo, malo amene Iye anawasankha kuti adzayikepo nsembeyo. Inu simungaiyike iyo pa chirichonse cha zipata izi; koma malo amene Iye anawasankha kuiyikapo iyo, Iye anaikanso Dzina Lake pa malo amenewo. Ndicho chimene Iye ananena apa. Iye anasankha kuyikapo Dzina Lake pamenepo. Tsopano tiyeni ife tifufuze Malemba a malo awa, pakuti amenewo ndi malo amene Iye anayikapo Dzina Lake.

¹⁰⁷ Tsopano tiyeni tiwerenge kuchokera pa mutu. Ndipo ine ndinali ndi kapepala kakang'ono kali apa kamene ine. . . mmawa uno, kabwera kwa ine. Tiyeni titenge ndime ya 2 ya mutu uwu. Tsopano, ine sindikufuna kukhala motalika kwambiri, chifukwa

cha anthu, pa kulumikiza uku kunja kuno. Tsopano ndime ya 2 ya mutu wa 16 uwu:

Inu muzipereka nsembe ya pasaka kwa AMBUYE Mulungu wanu, za nkhoa zanu ndi ng'ombe zanu, mmalo amene AMBUYE adzasankha kuyikapo dzina lake pamenepo.

¹⁰⁸ Tsopano, inu simungatenge ichi...kuwona mtima kwanu ndi zonse zimene inu mukufuna kuvomereza, inu simungayitengere iyo ku guwa la Methodisti, ku guwa la Baptisti, ku guwa la Chipentekoste, koma liripo guwa penapake pamene Iye anasankhapo kuti Iye...kuti adzayikepo Dzina Lake pamenepo, ndipo Iye akakumana nanu pa malo amenewo. Tsopano, ngati mutachipangitsa chirichonse kuti chiziyenda bwino, icho chiziyenda; chirichonse chiri mu dongosolo. Ngati mawayawo akugundana pamenepo, kuwala kumeneko sikungabwere; chifukwa iko kwakwiriridwa. Ndipo pamene inu mutenga amodzi a Mawu a Mulungu kapena amodzi a malo Ake, ndipo mu mtima mwanu momwe muli ndi zolinga zadyera, izo zidzakwirira mphamvu ya Mulungu pomwe apo. Ngati mukuchita zimenezo chifukwa mukufuna kukhala wanzeru, inu mukufuna kukhala wosiyana ndi winawake, kapena chinachake, pamenepo ikhazikika, iphulitsa fyuzi. Inu mukulakwitsa. Inu mukuyenera kubwera ndi kuwonamtima, ndi mtima wanu wonse, zolinga zanu ndi zokhumba zanu zitayikidwa kumene pa Mulungu. Mukatero mufufuze malo Ake, mupeze pamene Iye ananena, ndipo muzibweretse izo kumeneko. Mukuona?

¹⁰⁹ Tamuwonani Marita ndi Mariya. Pamene Yesu anabwerera, Iye atatha kuwaphunzitsa iwo Uthenga uwu (Kuwala kwa tsiku Lake, Iye pokhala Mesiya), Iye ankadedwa, anakanidwa. Oh, Afarisi ndi mipingo ankamunyoza Iye. Koma Lazaro anali atafa, m'bale amene anali bwenzi la pamtima kwa Iye. Iye anamulola iye kugona kumeneko; ndipo iwo anamuitana Iye, Iye sanabwere nkomwe.

¹¹⁰ Koma muwoneni Marita, khalidwe lake. Iye anati, "Ambuye, ngati Inu mukanakhala kuno." Mpatсени Iye udindo Wake woyenera: Ambuye, chilemba chachikulu A-m-b-u-y-e, *Yahweh*, Yehova. Ulemelero! "Ngati Inu mukanakhala kuno, mlongo wanga sakanafa." Moyo ndi imfa sizingagwirizane mu njira imodzi, kapena nyumba imodzi. "Inu mukana...Iye sibwenzi atafa."

¹¹¹ Yesu anati kwa iye, "Ine ndine chiukitsiro ndi Moyo," atero Mulungu. Mukuona? Pamene Iye anati, poyamba, "M'bale wako adzakhalanso ndi moyo."

¹¹² Iye anati, "Inde, Ambuye, ine ndikukhulupirira izo moona. Monga Myuda wamkazi, ine ndikukhulupirira kuti chidzakhalapo chiukitsiro cha akufa; ndipo ine ndikukhulupirira m'bale wanga anali wokhulupirika basi

ndi woonamtima mu kupembedza. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Inu ndinu Mesiya ameneyo, amene ananena mu Baibulo, chifukwa Mulungu akutsimikizira Mawu Ake mwa Inu zikuwonetsera kuti Inu ndi wa Mthenga wa ora lino. Inu ndinu Mesiya ameneyo. Ine ndikukhulupirira kuti Inu ndi Khristu ameneyo amene anali woti adzabwere, chifukwa ntchito Zanu zikuchitira umboni kuti Mulungu wakutumizani Inu kuno kuti mudzakhale Mesiya ameneyo.” Oh, mai! Penyani magudumu akuyamba kubwera mmalo mwake tsopano. Mukuona?

113 Tsopano, iye anali ndi ufulu woti, “Bwanji Inu simunabwere kudzamuukitsa m’bale wanga? Chifukwa chiyani Inu simunamuchiritse iye? Inu munachiritse ena. Bwenzi lanu lapamtima, ndipo taonani chimene chachitika.” Ayi, ayi, cholinga cha mtundu umenewo sichimafika paliponse.

114 “Ine ndikukhulupirira kuti Ndinu chimodzimodzi chimene Inu mukuzindikiritsidwa mu Lemba kuti muli. Ine ndikukhulupirira ili ndi tsiku limene Mesiya akuyenera kubwera; ife takhala tikuliyembekezera ilo. Ine sindikusamala zimene ena onsewo akunena. Ine ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse, ndi zimene ndaziwona ndi kumwa mwa Mawu, kuti Mawu akutsimikiziridwa mwa Inu, kuti Inu ndinu Mesiya ameneyo.” Mwaona, pansu mwa iye, iye—iye anali ndi chinachake choti afunse, koma iye ankayenera kubwera pa mpita woyenera.

115 Bwanji ngati iye akanathamangira kumeneko ndi kukati, “Ndiyeno Inu mukundiuzwa ine kuti Inu ndinu Mesiya ameneyo! Ndipo opanda ngakhale ulemu, njonda yokwanira kuyankha pempho lathu; pamene ife timakudyetsani Inu ndi kukusungani Inu mnyumba, ndi zonse, ndipo timakusamalirani Inu, ndipo tinasiya mipingo yathu, monga Inu munatilamulira ife kuti tichoke mu zipembedzo zimenezo.” Mukuona? “Ndipo apa ife tazisiya izo, ndipo tsopano ife tikuwerengedwa ngati otayika ndi zigawenga. Ndipo chirichonse chimene ife takuchitirani Inu, ndiyeno opanda ngakhale ulemu wamba kuti muyankhe kuyitana kwanga?” Tsopano, kwenikweni, iye anali nawo ufulu umenewo.

116 Monga inu mumanenera za tsitsi lanu lalifupi, “Ndine mzika ya Amerika. Ndikhoza kuvala akabudula, kuchita chirichonse chimene ndikufuna, si zoletsedwa.” Awo ndi maufulu anu, koma nkhoza nthawizonse imapinyolitsa maufulu ake. Uh-huh. Ngati ndinu mwanawankhosa! Iye samakhala ndi kalikonse koma ubweya, iye amawupereka iwo. Awo ndi maufulu ake opatsidwa ndi Mulungu, koma iye amawapinyolitsa iwo.

117 “Ine ndiri ndi ufulu wojowina chipembedzo chirichonse.” Ndiko kulondola ndendende, koma inu mumapinyolitsa zimenezo. Mukuona?

118 Iye anapinyolitsa zonse zimene iye anali nazo ufulu, kuti akawazindikire Mawu a Mulungu akuwonetseredwa pomwe apo

pamaso pake.

¹¹⁹ Iye anati, “Ine ndine chiwukitsiro ndi Moyo. Iye amene akhulupirira mwa Ine, ngakhale iye atafa, komabe iye adzakhala ndi moyo. Aliyense amene akhala ndi moyo ndi kukhulupirira mwa Ine sadzafa konse. Kodi mukukhulupirira izi?” Mwaona, apo panali gudumu limodzi laling’ono limene iye sanabwere nalo mu mzere. Mukuona?

¹²⁰ “Eya, Ambuye! Ine ndikukhulupirira kuti Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo!” O m’bale, chirichonse chinali chitakonzeka kuti chiyambe pomwepo. Mukuona?

¹²¹ “Kodi inu mwakamuyika kuti iye?” Mukuona? Ndipo inu mukudziwa chimene chinachitika.

¹²² Mwaona, inu mukuyenera kulowa mmalo oyenera amenewo Iye asanalandire nsembe yanu. Mwaona, mukuyenera kubwera mwa iwo. Tsopano, penyani.

. . . pamalo amene AMBUYE adzasankha kuikapo dzina lake.

Inu musadye mkate wa chotupitsa mwa iwo; . . .

¹²³ Kodi zimenezo zimaimira chiyani mu nsembe? Musasakanize izo ndi kachikhulupiriro kalikonse, izo zikuyenera kukhala Mawu. “*Popanda mkate wa chotupitsa.*” Chotupitsa ndi . . . Inu mukudziwa chimene chotupitsa chiri mu chirichonse. “Chotupitsa pang’ono chimatupitsa mtanda wonse,” mtanda wonse ndi Thupi. Inu simungayike chidutswa chimodzi cha chipembedzo kapena kachikhulupiriro mwa Khristu. Ayi, bwana, sizingagwire ntchito.

¹²⁴ Inu mukukumbukira uthenga wa Lachinai lapitali usiku? Mwamuna wanu wakale akuyenera kuti afe. Uko nkulondola. Mwamuna wanu watsopano ndi Mawu.

. . . masiku seveni inu mudzadya mkate wopanda chotupitsa mnenemo, . . .

¹²⁵ “*Masiku seveni,*” kodi zimenezo zikuimira chiyani? Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo yathunthu, masiku seveni. Nchifukwa chiyani ankayenera kudya iwo masiku seveni? Pasanachitike chiyani? Asanatuluke kumeneko. Ndipo m’badwo wa mpingo wonse, kuchokera pachiyambi mpaka kumapeto, ukuyenera kukhala moyo pa Mawu a Mulungu a m’badwo umenewo. Chotero kachikhulupiriro kanu ka Chiroma, Methodisti, Baptisti, ndi kachikhulupiriro ka Chipentekoste zonse ndi zakufa.

¹²⁶ Tsopano penyani.

. . . mnenemo, ngakhale mkate wa msautso; . . .

Anazunzidwa chifukwa cha Iwo; Luther, Wesley, Achipentekoste; onse anazunzidwa, chotero inunso mudzatero.

...pakuti inu munaturuka mdziko la Igupto mwamsanga...inu mudzatsalira tsiku limene... kumbukirani tsiku limene munaturuka mdziko la Igupto masiku onse a moyo wanu.

Ndipo sipadzawoneka mkate wa chotupitsa mu...ndi inu mmalire anu onse masiku seveni;...

¹²⁷ Mwa Mkwatibwi wokongola wa Khristu, itachitika imfa Yake kudutsa Mibadwo Yamdima ndi ufumu wa Chiroma, kuti Iye ankayenera kufa, “pokhapokha njere ya tirigu itagwera mu nthaka.” Mkwati ankayenera kuti abwere, Mbambande yangwirowo ya Mulungu. Inu nonse munamva uthenga wanga pa izo.

¹²⁸ Ine ndinaima kutsidyako, Los Angeles, ku Forest Lawn, tsiku lina, ndipo mtima wanga unalumpha. Ndi angati amene anakhalapo ku Forest Lawn? Kuli a...chosedwa cha Mose ndi—ndi...-angelo, ine ndikukhulupirira ndi choncho, Michelangelo. Ndipo ndi chosedwa changwirowo, zonse kupatula pa bondo lakumanja; pali kabala pafupifupi kuya kwa theka la inchi. Ndipo wondilondolerayo...Ine ndimayang’ana, ndipo iye analozera izo kwa ine. Iye anati, “Michelangelo anakhala moyo wake wonse akuyesetsa kuti—apange...Iye anali wosema, ndipo iye anali kuyesetsa kuti apange chifano cha Mose. Kumbuyo mmaganizo mwake, iye anali akulingalira mmene Mose ankayenera kuwonekera. Iye anali nacho icho mu mtima mwake, momwe Mose ankayenera kumawonekera. Ndipo kenako iye anakhala moyo wake wonse; akugoba pang’ono apa, ndi kumakhula icho, kuyima mmbuyo ndi kudzayang’ana pa icho. Chaka ndi chaka, iye ankagwira ntchito pa icho. Potsiriza pamene icho chinamalizidwa, ndipo iye nabwerera mmbuyo ndipo nayika panso sanza yake ndi hamala yake, iye anayang’ana pa chosemacho. Icho chinali changwirowo kwambiri chifano cha Mose chimene iye anali nacho mu mtima mwake, mpaka iye anabalalika kwambiri, iye anatenga hamala ndipo anachikantha icho, nafuula, ‘Yankhula!’” Icho chimatchedwa *Mbambande ya Michelangelo*. Chinachake chachikulu chija mwa wosema uja, masomphenya aja amene iye anali nawo a chimene Mose amayenera kukhala nacho, zinali kungowonetsera mwa choyimira cha Atate Mulungu wamkulu.

¹²⁹ Iye anali nacho mu mtima Mwake, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, Mwana, chifukwa Iye ndi Atate. Koma izo zinali mu nyongolosi za Mawu Ake. Ndipo Iye anamlenga munthu, ndipo Iye anamuyika iye pa ufulu wosankha, koma munthu ameneyo anagwa. Koma Wosema wamkuluyo, Mulungu, amene anampanga munthu ndi fumbi la mnthaka, Iye sanakhazikike pa zimenezo, Iye anayambanso kumupanga munthu. Ndipo Iye anamupanga Nowa, iye anafa ataledzera. Iye anamupanga Mose amene analephera kusunga Mawu Ake. Iye anapanga aneneri amene amathamanga mu nthawi ya mavuto.

Ndipo Iye anali kupitiriza kumamanga ndi kumawumba mpaka patapita kanthawi Iye ankafuna m—mbambande, kuti ikamunyezimiritse Iye, chikhalidwe Chake, chimene chinali mu mtima Mwake chimene mwana akuyenera kukhala.

¹³⁰ Tsiku lina, kumusi ku Yordani, Mbambande imeneyo itatha kuwumbidwa ndi kupangidwa, apa Iye anabwera akutsika mu a...pa mapiko a Nkhunda, anati, “Uyu ndi Iyeyo!” Iye anakondowededwa kwambiri ndi Mbambande iyi mpaka Iye anamukantha Iye pa Kalvare, kuti Iye adzatifere ena tonsefe opanda ungwiro; kuti kudzera mu kukhetsa kwa Magazi Ake, Iye akakhoze kubweretsa mbambande zambiri (kukhala Mkwatibwi) kwa Mwana Wake. Mbambande ili ndi chipsyera chifukwa cha kukondowedeka kwa Mulungu ataiwona Mbambande yoteroyo, Iye anamukantha Iye chifukwa cha ife tonse. Mukuona? Pamenepo Iye anafa, kuti adzatipangitse ife kukhala ungwiro amene tinali opanda ungwiro. Mbambande.

¹³¹ Zindikirani, umu apa Iye anati:

*...masiku seveni inu mudzadya mkate uwu wopanda
chotupitsa...*

¹³² Tsopano, mkate umafaniziridwa. Yesu anati, “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse.” Osati basi—Mawu okha apa ndi apo monga zipembezozingakuchititsireni inu kuwakhulupirira Iwo. Koma Mawu a Mulungu ndi ungwiro! Ndi Mulungu Mwiniwake mmawonekedwe a kalata, wotchedwa “Mbewu.” Ndipo mtundu woyenera wa chikhulupiriro chosapitsidwa mu Mawu amenewo udzabweretsa Mbewu imeneyo ku Moyo wake.

¹³³ Ndizo ndendende zimene inu mumaziwona usiku mu kuzindikira za mmitima, ndi zinthu zina zonse izi, chifukwa ilo ndi lonjezo limene Mulungu anapanga. Ndipo Iye anayima pafupi ndi ine ndipo anandiuza ine zimenezo, ndipo anandiuza ine “onyenga awa adzauka, koma ugwiritsitse mokhazikika.” Ine ndikuwakhulupirira Iwo. Ndipo palibe zolinga zadyera, kuti ndimuvulaze alyense, koma kukhala wolemekeza kwa Mulungu ndi kuchita ntchito imene Iye anandiyitanira kuti ndiichite, ndi chifukwa chimene ine ndimanena zinthu izi. Ndipo Mulungu amazitsimikiziranso izo, ndipo amalandira choperekacho ndi nsembe, potsimikizira izo kukhala Choonadi. Palibe funso kwa Iwo! Tsopano penyani Mawu amenewo!

¹³⁴ Tsopano, ife tikuzindikira apa, “*Masiku seveni,*” izo ndi za kwa m’badwo wa mpingo uliwonse. Tsopano, monga Mbambande iyo inkayenera kufa, kuti iwukitsidwe kuti itiwohole ife tonse. Zitatero Iye anakhala ndi mpingo utayikidwa mu dongosolo pa Pentekoste, koma Mpingo umenewo unyakenera kuti udutse mu nsembe; ndipo dziko la Chiroma linawupha iwo, linawuyika iwo mu nthaka.

¹³⁵ Monga mlembi wa bukhu ili, sindingathe kuganizira za ilo tsopano, anapanga kusereula kochulukwa kwa ine, ndipo anati, “Mwa adierekezi onse, ndi William Branham.” Mwaona, ndicho chimene mdierekezi amayesera kunena. Iye anati, “Masomphenya ndi zinthu,” anati, “zimenezo ndi za mdierekezi,” iye anati, “kapena, iye ndi mtundu wina wa wopepetula, kapena akugwira ntchito mu kuzindikira kwapamwamba.” Dziko laluntha nthawizonse likuyesetsa kuwalingalira Iwo.

¹³⁶ Ndi kumene iwo anayesera kumulingalira Yesu. “Mumachita motani zinthu zimenezi? Nchiyani chinachita izo?”

¹³⁷ Iye anati, “Ndikufunsani inu funso. Kodi utumiki wa Yohane M’batizi. . . Kodi iwo unali wa Mulungu kapena unali wa munthu?” Mukuona?

¹³⁸ Anati, “Ife sitingathe kunena.”

¹³⁹ Anati, “Inenso sindikuuzani inu.” Uko nkulondola. Iwo anapitirira. “Kuchokera pamenepo palibe munthu anamufunsa Iye chirichonse.” Mukuona? Iye anangowadulapo iwo, Iye sanawauze iwo kalikonse ka Iwo; sizimawakhudza iwo. Iye anali ndi ntchito yoti ayichite ndipo Iye anaimalizitsa iyo.

¹⁴⁰ Mulungu atithandize ife kuti tizichita chinthu chomwecho. Ife sitikusowa kuyankha funso la mdierekezi, uko nkulondola, “Ngati inu muli, chitani *chakuti ndi chakuti*.” Inu muli ndi udindo pa Uthenga umenewo, mlaliki ali, ndipo ndizo zonse; osati momwe Iwo analembedwera, ali ndi udindo wonena Izo basi.

¹⁴¹ Ndipo monga wantchito, ngati iwe uli mneneri, iwe umakhala ndi udindo kwa Mulungu. Ndipo ngati masomphenya amene amabwera apepuza Lemba ili ndi kusonyeza chimene Ilo ili, iwe umakhala ndi udindo pa Mawu aliwonse amene ali mu Baibulo limenelo, chifukwa Iwo onse analembedwa ndi mtundu womwewo wa anthu amene inu muli. “Mulungu wakale ankasuntha, mwa aneneri, ndipo analemba Lo- . . . Baibulo Lopatulika.” Mukuona? Ndipo palibe mneneri weniweni wa Mulungu angakane Mawu amodzi a Iwo, koma kukhulupirira Mawu aliwonse ndi kulalikira mofanana. Ndiyeno Mulungu amakhala wokakamizika kuchokera mu mpita umenewo kuti awapangitse Mawu amenewo kukwaniritsidwa ndendende basi momwe Iwo analonjezedwera, Mbewu idzakula.

¹⁴² Tsopano, zindikirani kenanso, mwamsanga, ife tikupeza apa kuti masiku seveni onse amene mkate uwu unali woti udyedwe, kudutsa mu Mibadwo Ya Mpingo Isanu Ndi Iwiri. Tsopano, pamene iwo un kayenera kufa ndi kulowa mu nthaka.

¹⁴³ Ndipo wotsutsa uyu amene amalankhula za ine, anati, “Za Mulungu amene anthu inu mumamupembedza, amene amakhoza kukhala mu Mibadwo ya Mdimu ndi kumawawona amayi amenewo, oyembekezera, ena a iwo ali ndi ana aang’ono

mmanja mwawo, anthu odzipereka, kuponyedwa mu bwalo ndipo mikango nkuwakhadzulira iwo mzipidutswa, ndipo iwo akufuula; kuwapachika iwo pa mitanda ndi kuwawotcha iwo; kuwavula akazi maliseche, anamwali aang'ono, ndi kudziponya okha mmbuyo monga *chonchi*, ndi kudzaimasulira mikango pa iwo." Anati, "Mulungu amene amakhoza kukhala Kumwamba, ayenera kuti amakhala pa mpandowachifumu Wake, ndipo amayang'ana pansi ndi kumanena kuti Iye amasangalala nazo," anatero.

¹⁴⁴ Ndiye, mwaona, kumeneko ndi kulingalira kwaluntha kumene kuli kwa mdierekezi. Ngati munthuyo akanakhala wauzimu, iye akanadziwa kuti njere ya tirigu ija imayenera kufa, iyo imayenera kuyikidwa mmunda mu kafidulo ya Chiroma.

¹⁴⁵ Komano mphukira yaying'ono yoyamba ya Moyo inatulukira mu kukonzanso ndi Martin Luther, kuti, "Olungama sadzakhala moyo ndi kokulumunya kodala kamene wansembe amachita, koma mwa Mawu a Mulungu. 'Olungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro!'" Iye anayika mmwamba timitengo tiwiri. Mbewu ya tirigu inayamba kukula.

¹⁴⁶ Kenako motsatira panadzabwera John Wesley ndipo anadzawonjezera kwa izo. (Panali ena ambiri, amene... Zwingli ndi iwo anadzabwera ndipo anakana kubadwa kwa namwali, ndipo izo zinangofera pansi.) Koma motsatira panadza Amethodisti, ngayaye, mungu, tsiku la umishonare. Ndipo iwo ankalalikira kuyeretsewa; anawonjezera ngayaye.

¹⁴⁷ Kenako motsatira panadza Achipentekoste mu mankhusu, mochulukwa kwambiri, kuti adzanyenge Osankhidwa. Zinkawoneka ngati njere yeniyeni ya tirigu, itatsegulidwa, munalibemo tirigu nkomwe. Koma Moyo ukudutsa mu mankhusu.

¹⁴⁸ Tsopano, kodi munazindikira, zaka zitatu zirizonse ukatha a—msonkhano waukulu, chimachitika ndi chiyani? Chipembedzo. Izi ndi zaka twente ndipo palibe chipembedzo. Wokonedwa Mwanawankhosa wakufa, mulole izo zisachite konse zimenezo. Ngati ine ndingapite mu kam'badwo kano, mulole anthu amene akukhulupirira Uthenga uwu asadzayime konse ndi chipembedzo! Mulungu adzatero... Inu mudzafa mu njira yanu! Mukumbukire zimenezo! Ora lomwelo limene inu mudzatchule chipembedzo pakati panu, ine sindikusamala kaya ndinu odzipereka bwanji, kumutenga munthu kukhala mtsogoleri wanu mmalo mwa Mzimu Woyera kuti azitsimikizira Mawu awa, limenelo ndi ora limene inu mudzafa! Mbewu yeniyeni siingatero, chifukwa palibe kanthu katsalira pambuyo pa mbewu, ndi chinthu chomwecho chimene chinali mmbuyo pachiyambi. Ndi Mkwatibwi amene anagwera mu nthaka kuti abalenso mbewu ya tirigu.

¹⁴⁹ Zindikirani:

...masiku seveni inu mudzadya mkate wopanda chotupitsa...

150 Ndipo kumeneko adzakhala ndi Mkwatibwi...

151 Tsopano, inu anthu amene munali ndi mayi wa Methodisti wofuula uja, ndi zina zotero, kuti inu munkadabwa “Ngati iye sanayankhule mmalirime, iye sakakhalako kumeneko.” Limenelo ndi bodza! Iye anali Mzimu Woyera womwe uja umene inu muli nawo lero, koma iwo unali mmawonekedwe a ngayaye, osati kubwezeretsa kwa mphatso. Koma masiku seveni onse, muzingodya mkate wopanda chotupitsa, Mawu. Iwo, mmbuyo, iwo amene anachita chipembedzo, anafa. Iwo ndi phesi, iwo adzangosonkhanitsidwa ndi kuwotchedwa. Koma Moyo ukupitirirabe. Ndipo chimachitika ndi chiyani? Moyo wonse umene unali mu phesi, mu ngayaye, mu mankhusu, wonse ukudzathera mu tirigu. Ndipo Mzimu Woyera womwewo umene unamubweretsa Luther, unamubweretsa Wesley, unawabweretsa Achipentekoste, ukudzathera mwa Mkwatibwi pa chiukitsiro.

152 “Masiku seveni, muzidya mkate wopanda chotupitsa.” Palibe chotupitsa chomwe chidzapezeke pakati pa Mkwatibwi, ayi—popanda mawu owonjezera, popanda kalikonse. Kumbukirani, mawu amodzi anayambitsa imfa iliyonse imene ilipo mdziko lapansi; mwana aliyense wapathengo anabadwa chifukwa Eva, mpingo woyamba, mkwatibwi wa Adamu woyamba, anakaikira Mawu a Mulungu ndipo anavomereza chipembedzo, kapena luntha, kapena kuchotsapo sukulu ya Iwo; chifukwa Iwo anaganiziridwa, kuti, “Ndithudi, Mulungu ndi Mulungu wabwino.” Mulungu ndi Mulungu wabwino, komanso Iye ndi Mulungu wolungama. Tikuyenera kusunga Mawu Ake! Sukulu, iye anavomereza izo.

153 Kumeneko ndi kumene ena a inu anyamata akuseminare, sindikukaika muli nako kuyitana mmoyo wanu, koma inu munathamangira ku sukulu ina ya Baibulo kuti akakubaireni chiphunzitso ichi mwa inu, ndipo pamenepo ndi pamene inu munafera...Mukhale ndi Mulungu ndi Mawu Ake. Iwo sangakuloleni inu; kapena, inu simungakhale a osonkhana awo, sangakulandireni inu pa nsanja. Chotero asiyei iwo akhale nacho, asiyei akufa ayikane akufa, tiyei timutsatire Khristu Mawu.

154 Tsopano, masiku seveni sipadzakhala chotupitsa chiti chidzasakanizidwe mwa Mkwatibwi, Mpingo, masiku seveni.

155 Tsopano zindikirani. Tsopano ngati opanda...

Ndipo pasadzawoneke mkate wa chotupitsa mwa iwe mmalire ako onse masiku seveni;... (Nsembe apa ndi choyimira: Mkwatibwi akutulukira kuchokera ku Nsembe imene ili Khristu.) ...komanso sipadzakhala

*chirichonse cha mnofu, chimene inu munapereka
nsembe tsiku loyamba madzulo, . . .*

156 Ndipo mukukumbukira—mukukumbukira momwe ife tangodutsa kumene mu Mibadwo ya Mpingo? Wa mthenga kwa mpingo nthawizonse amabwera pa kufa kwa m'badwo wa mpingo winawo, nthawizonse. Kufa kwa Pentekoste kukubweretsa mkwatulo wa Mkwatibwi. Mukuona? Kufa kwa Luther kunabweretsapo Wesley. Mukuona? Kufa kwa Wesley kunabweretsa Pentekoste. Kufa kwa Pentekoste kukubweretsa Uthenga tsopano. Apa, izo ziri pomwe apa, zokonzedwa kudutsa monse mu Lemba. Palibepo lemba mu Baibulo koma limene limalumikizana lina ndi limzake. Mukuona? Zoyimira zonse izi. Ine ndiribe maphunziro, koma ndiri nawo Mzimu Woyera umene umandiwonetsa ine kudutsa mu mpita wina kuti ndiphunzitse izo kuchokera, kuchokera ku chirengedwe; ndipo ndizo mwa Mawu. Akuyenera kukhala Mawu, zinthu zinalonjezedwa.

*. . . thupi, . . . nsembe tsiku loyamba . . . ngakhale,
mudzakhale usiku wonse mpaka mmawa.*

157 Tsopano, ngakhale Luther, amene anali ndi Choonadi ndipo ankawuphunzitsa mpingo “olungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro.” Inu simufuna kukangamira ku zimenezo kukhala chiphunzitso chathunthu, mu m'badwo wa Methodisti. Kodi inu mudzachita chiyani? Ziwotcheni izo ndi moto. Kodi chinali choyimira cha chiyani? Chipembedzo chimene chimatuluka mu Mawu amenewo ndi mankhusu, phesi, mankhusu, chikuyenera kuwotchedwa ndi moto. Gawo lachipembedzo lija limene icho chinadutsamo silikuyenera kutsala, likuyenera kufa. Musachisiye icho mpaka kusweka kwa wina—m'badwo wina, chitentheni icho! Iye akuyankhula tsopano kwa Mkwatibwi apa, Mkwatibwi yekha, akubwera kudutsa mu m'badwo uliwonse.

158 Zindikirani kukongola kwake, “Magazi a mwanawankhosa.” Awa ndi Thupi la Khristu, Nsembe: magazi a mwanawankhosa pakhomo. Tsopano, kumbukirani, mwanawankhosa anaphedwa chimene chinali choyimira cha Khristu.

159 Kapena tikhoza kutenga nthawi yambiri, koma ine ndiribe . . . maminiti pang'ono ena chabe kuti tikhalepo apa. Ine ndikhoza kungoyimikira ndi kudzayambiranso usikuuno, mwaona, chifukwa ife tikutalikitsa kwambiri. Ndi . . . Ine ndiri ndi masamba twente a izi apa, za zolemba, pa phunziro limodzi ili.

160 Zindikirani tsopano, pa izi, a—mwanawankhosa anali Khristu mophiphiritsa. Kapena kodi ndanena izo molondola? Moyimira; Khristu anali Mwanawankhosa. Iye ankayenera kukhala wamwamuna, woyamba kuchokera kwa nkhusa yayikazi yayikulu; kapena nkhusa yayikazi, chirichonse chimene mungasankhe kuitchula iyo. Iye akuyenera kukhala woyamba

wake. Ndipo akuyenera kuyesedwa poyamba kuti awone ngati ali ndi chirema.

¹⁶¹ Tsopano, Khristu anayesedwa; mwanawankhosa woyamba wa nkhosa yayikazi, Maria namwali. Ndipo anayesedwa ndi chiyani? Satana akutsutsa Mawu. Pamene iye anamumenya Eva, iye anagwa; anamumenya Mose, iye anagwa; koma pamene iye anadzawulukira m'mwamba nkudzamutsutsa Khristu, ndi kudzayesera kubwereza Lemba kwa Iye molakwika, uh-huh, iye anapeza kuti ameneyo sanali Mose. Mukuona? Iye anayesedwa. Anachita chiyani. . . iye anatembenuka, ndipo anati, “Ngati Inu muli Mwana wa Mulungu. Tsopano iwo amandiuza ine kuti Inu mumachita zozizwitsa, ndipo iwo amandiuza ine kuti Mesiya ndi woti adzachite zimenezo. Tsopano, ngati izo ziri, Inu muli ndi njala, Inu simunadye, sandutsani mikate iyi kukhala, kapena, miyala iyi kukhala mkate, ndipo mudyee.”

¹⁶² Iye anati, “Kwalembedwa, ‘Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha.’” Kachikhulupiriro kanu, zina zotero. Koma ndi chiyani? Mawu aliwonse! Gawo la Mawu? “Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Ndicho chimene munthu amakhalira moyo. Mukuona? Mwanawankhosa anayesedwa, kuwona ngati pali paliponse pamene Iye anagwa.

¹⁶³ Afarisi, “O Rabbi, Inu Mneneri wamng’ono, ife tikuganiza kuti Ndinu wodabwitsa. Ndinu wabwino.”

¹⁶⁴ “Bwanji ukunditcha Ine wabwino? Pali Mmodzi yekha wabwino, ndipo ameneyo ndi Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira izo?”

¹⁶⁵ “Oh, inde. Mulungu.”

¹⁶⁶ “Chabwino, Ine ndine Iye, ndiye.” Uh-huh. “Inu munati alipo Mmodzi yekha wabwino. Munditchuliranji Ine ‘wabwino,’ pamene simukukhulupirira kuti ndine Mulungu?” Uh-huh. “Ndiye nchifukwa chiyani mukunditchula Ine wabwino? Nchiyani chikukupangitsani inu kuchita zimenezo? Nchiyani chinakukondowezani inu kunena zimenezo, pamene inu mukudziwa kuti pali wabwino mmodzi yekha, ndipo ameneyo ndi Mulungu?”

¹⁶⁷ “Ife tikudziwa kuti Inu simulemekeza ulemu wa munthu kapena mawu a udindo wawo. Ife tikudziwa zimenezo.” Yeserani. . . Iye ankamudziwa wachinyengo ameneyo. Mukuona?

¹⁶⁸ Iye anayesedwa kuti awone pamene Iye anayima, mwaona, anayesedwa mu njira iliyonse, anayesedwa monga momwe ife timayesedwera. Koma panalibe kugonja, kwa Iye, nkomwe. Ayi, bwana! Ameneyo anali Mwana wa Mulungu.

¹⁶⁹ Ndipo mwanawankhosa anayesedwa, ndipo anasungidwa kwa masiku fortini. Amenewo anali Masabata awiri, kapena mibadwo iwiri. Umodzi wa Ayuda, umene iwo ankapereka mwanawankhosa mwa choimira; umodzi ndi wa Amitundu,

amene ali ndi Mwanawankhosa weniweni, ndipo onse a iwo anapangidwa angwiro pokhulupirira kuti Mwanawankhosa uyu adzabwera. Koma Iye anayesedwa fortini... kapena kufufuzidwa masiku fortini, Iye anali Mawu.

¹⁷⁰ Ndipo inu mukhoza kufufuza Chipangano Chakale, kunena “Izo zimatsutsa Chatsopano.” Inu mukulakwitsa! Chipangano Chakale chimangochitira umboni za Chatsopano.

¹⁷¹ Munthu ankati anditsutse ine osati kale kwambiri, anati, “Chavuta ndi chiyani ndi iye?” Anati, “Chabwino, iye amaphunzitsa ngakhale kuchokera mu Chipangano Chakale.” Mlaliki wa Chikhristu, taganizani za izo. Anati, “Chipangano Chakale chinafa ndipo chinapita.” Oh, ayi! Oh, ayi! Ndi mphunzitsi wasukulu chabe, kuti atiwonetse ife chimene chalembedwa pa khoma. Mukuona? Uko nkulondola.

¹⁷² Tsopano, mwaona, masiku fortini iwo anayesedwa, ameneyo anali Khristu. Tsopano zindikirani, ndiye iye ankaphedwa nthawi yamadzulo, akuyenera kuphedwa, mwanawankhosa amatero. Khristu anafa mu nthawi yamadzulo, masana. Ndiyeno zindikirani, ndiye iye analinso...

¹⁷³ Magazi anali oti ayikidwe pa mphuthu za zitseko, mwaona, chimene magazi ndi moyo wa nyama. “Inu muzidya nyama yake; koma mwazi wake umene uli moyo, muwutaye iwo.” Mukuona? Iwo ankayenera kukhala... Magazi ankayenera kuyikidwa pa mphuthu za nyumba imene nsembe yalandilidwayo. Ulemelero! Kodi Moyo ndi chiyani? Dzina. Kuti... Iye ankayika dzina la munthuyo... Pitani pa khomo, ndipo mukawone, mukawone dzina limene liri pakhomo inu musanayimbe belu. Mukuona? Magazi anaikidwa pa mphuthu ya chitseko ngati choyimira cha chimene nsembe inali mkatimo.

¹⁷⁴ Tsopano ife tipeza malo opembedzera, kupyola pamenepo, kubwera kupyolera mu Magazi amenewo. Zindikirani, magazi pa chitseko ankayankhula dzina la chimene chinali kuchitika... anali mkati, iwo anali mmenemo. Malo athu opembedzera, Mwanawankhosa, ndi Mawu. Ife tikudziwa zimenezo.

¹⁷⁵ Tsopano, ndime 4, zindikirani, “Musasiye mkate, musasiye chirichonse cha nsembe,” kapena, kumutenga wina kuchokera ku m’badwo wina kupita naye kwa wina.

¹⁷⁶ Kuyesera kubwerera mmbuyo ndikuti, “Chabwino, tsopano, ndife Achilutera, ife tikufuna kubwera kuno,” inu mukuyenera kuti mufe ku m’badwo wa Chilutera kuti mubadwire mu m’badwo wa Wesley. Inu mukuyenera kufa mu m’badwo wa Wesley kuti mubadwe mu m’badwo wa Chipentekoste. Ndipo inu mukuyenera kuti mufe mu m’badwo wa Chipentekoste, osasiya kalikonse ka iwo kotsalira, muwotche ndi moto, chifukwa iwo udzawotchedwa ngati phesi limene tirigu amachokerapo. Phesi, chipembedzo, ilo likuyenera kuwotchedwa. Chotero musabweretse chipembedzo chanu mu Uthenga watsopano. Awa

ndi Mawu tsopano. Ndicho chimene chinapanga chipembedzo, phesi; ilo linanyamula Iwo, ndiko kulondola; koma Iwo anabwera cha *kuno*, kenako phesilo linafa. Icho chinali chonyamulira, chipembedzo, koma Mawu akupitirirabe. Eya, Mawu akupitirirabe.

¹⁷⁷ Tsopano tengani ndime ya 5 ndi ya 6. Zindikirani, “Ayi. . .” Tsopano tiyeni titenge ndime ya 5 ndi ya 6.

*Musamapereke msembe mu zipata zirizonse, zimene
AMBUYE Mulungu wanu wakupatsani:*

¹⁷⁸ Tsopano kumbukirani, “Osati mu chirichonse cha zipata zimenezi.” Ambuye amakulolani inu kuti mukhale ndi zipembedzo izi, mwaona, “zipata izi.”

*Koma pa malo amene AMBUYE. . . Mulungu adzasankha
kuikapo dzina lake, . . .*

¹⁷⁹ Ndicho Chipatacho, malo okhawo. “Osati mu chirichonse cha zipata izi.” Koma Mulungu ali ndi Chipata.

¹⁸⁰ Inu mukuti, “Mmawa uliwonse ndimalowa pachipata cha Methodisti.” Umenewo ndi mpingo. “Mmawa uliwonse ndimapita ku chipata cha Katolika.” Uh-huh. Chabwino, Ambuye anawalola anthu Ake kuti alowe ndi kutuluka pa zipata zimenezo. Mulungu ali nawo anthu mu mpingo wa Katolika, mpingo wa Methodisti, mpingo wa Presbateria, yonse ya imeneyo, Achipentekoste. Ndithudi, koma musati. . . inu musakapembedze Ambuye pa chipata chimenecho. Mukuona? Koma Ambuye ali ndi chipata chinachake. Ulemelero! Iye ali ndi chipata.

*Koma pa malo amene AMBUYE Mulungu wanu. . .
wasankha kuti ayikepo dzina lake, pamenepo. . . inu
mudzapereka nsembe pasaka madzulo, . . .*

¹⁸¹ Kodi ndi liti limene Rebeka anamupeza Isaki? Ndi liti limene Eliezara anamuitana iye kuti akhale mkwatibwi? Nthawi ya kumadzulo!

Kudzakhala Kuwala nthawi ya kumadzulo,
Njira ya Ulemelero ndithudi mudzaipeza;
Mu njira yamadzi imeneyo muli Kuwala lero,
Kuyikidwa mu Dzina lofunika la Yesu;
Ana ndi aakulu, lapani machimo anu onse,
Mzimu Woyera udzalowamo ndithudi;
Kuwala kwa madzulo kwabwera,
Ndi zoonza kuti Mulungu ndi Khristu ndi
Mmodzi.

¹⁸² Chimenecho chinali chiyambi cha Iwo, tsopano iye wazimirira mpaka mu Kuwala kwa Mkwatibwi. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

¹⁸³ Ine kulibwino nditseke apa, ndiyambiranso usikuuno, chifukwa ine sindikufuna kuti inu musiye izi, inu mwaona.

Ayi, ayi ndi—ndi nthawi ya chakudya chamadzulo. Chabwino, chabwino, ine ndiri ndi zolembe zambiri zimene ndinalemba apa. Oh, mai! Nanga bwanji usikuuno, izo zingakhale bwino? [Osonkhana akuti, “Ayi. Tsopano.”—Mkonzi]. Huh? Chabwino, ngati inu. . . Inu mukufuna kungoyesera patsogolo pang’ono? [“Inde. Amenii.”] Chabwino, tiyeni tipite patsogolo pang’ono ndiye, tifulumira mwachangu. Izo ziri bwanji?

¹⁸⁴ Tsopano, kulowa mu chiyani? “Musamalowe pachipata chirichonse chimene Ambuye Mulungu wakupatsani inu, koma pa chipata chimene Ambuye adzayike Dzina lake.” Osati kulowa mu nyumba ya—ya chipata chimene chiri chitseko. Nkulondola uko? Mulungu adzayika Dzina Lake pakhomo, ndipo inu simudzatero. . . Ndicho chipata cholowera ku malo opembedzerapo, malo opatulika. Inu musakalowe pamenepo ndi nsembe yanu ku chirichonse cha zipata izi, koma pa chipata chimene Ambuye Mulungu wasankha kuti ayikepo Dzina Lake. Mukuona?

¹⁸⁵ Tsopano, kodi Iye anachita zimenezo? Chipata chimenecho chiri kuti? Mu Yohane Woyera 10, Yesu anati, “Ine ndine Chipata, Khomo. Ine ndine Khomo la Nyumba ya Mulungu. Ine ndine Khomo ku khola la nkhosa.” Osati khola la mbuzi, khola la nkhosa. Mukuona? “Ine ndine Khomo ku khola la nkhosa. Munthu akhoza kulowa pa Khomo ili, nkukhala wotetezeka.”

¹⁸⁶ Ndipo tsopano ife tikhoza kukhala kwa nthawi yayitali pa izo. Koma, kuti tisunge nthawi, Iye ndi Khomo ku khola la nkhosa limenelo. Tsopano, tikufuna kuzindikira apa, mithunzi ndi zoyimira zikuwonekera kwenikweni apa, koma ine. . . ngati ndingatenge tsamba limenelo ndinga. . . ndikusungani inu kwa kanthawi.

¹⁸⁷ Chabwino, zindikirani, izi zikubweretsamo mawonekedwe angwiwo, Yesu Khristu. Pakuti Chipangano Chakale chonse ndi choyimira cha Iye, maphwando onse, kupembedza konse, ndi chirichonse. Ndipo ine ndazilemba apa, pansi pa mzere wa Malemba awa, “Kufotokoza izo.” Kumeneko ndi kumene izo zingatenge nthawi yayitali. Kufotokoza mmene maphwando onse. . . Ngakhale nsembe ya ufa inali choimira cha Khristu. Tiyeni tingoyitenga iyo.

¹⁸⁸ Nthawi ina panali a—sukulu yotchedwa sukulu ya atumiki, kapena sukulu ya aneneri. Iwo anaphunzitsidwa, aneneri ophunzira. Ndipo kunali mneneri weniweni, woyitanidwa ndi Mulungu nthawi yina anapita uko kuti akawachezere iwo. Chabwino, iwo ankafuna kumuwonetsa mneneri wokalambayo ulemu pang’ono, chotero mmodzi wa iwo anatuluka ndipo anatenga mulu waukulu wa chimene iye ankaganiza kuti ndi nandolo; koma izo zinali mphonda zachiphe, ndipo iye ankati awadyetse iwo onse zimenezo.

189 Oh! Ndi akuseminare apang’ono angati amene ife takhala nawo! Mukuona? Kulondola. Iwo akuphika chinachake. Mukuona? Iwo ali ndi a Methodististi apang’ono, a Baptististi apang’ono, a Pentekoste apang’ono. Koma, inu mwaona, izo ndi mphukira yachiwiri, mtundu umene ungamulidwe kuchokera pa mtengo. Mwaona, osati mu Mpesa waukuluwo. Ukubereka mandimu, mphesa, ndi zina zotero; osati malalanje, koma kudzinenera kuti ndi zowawasa.

190 Zindikirani kenanso. Tsopano, mu izi—mu izi, pamene Eliya anabwera mozungulira ndi kudzayang’ana pa iwo, ndipo nawona kuti zinali mphonda zachiphe zimene zikanapha aliynse wa iwo, iwo anati, “Kalanga, ife tiri ndi imfa mu m’phika!”

191 Iye anati, “Ndibweretsereni ufa wodzaza dzanja.” Ndipo anaponyeramo ufa mmenemo, iye anati, “Tsopano ziri bwino, idyani zimene mukufuna.” Iwo unasintha imfa kukhala moyo.

192 Ndipo nsembe ya ufa imene inaperekedwa kwa Khristu. . . Iye anali nsembe ya Ufa, ndipo nsembe yaufayo ikuyenera kuperedwa ndi chitsulo chinachake chimene chinapanga gawo laling’ono lililonse la ufawo kufanana, zikusonyeza kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye ali chinthu chomwecho choti muyike mu chipembedzo chanu ndipo icho chidzakhala moyo: Mawu! Khristu ndi Mawu, zoyimira zonse za chirichonse: kachisi, a—a—mkate wopanda chotupitsa, chirichonse. Mkate wonyemedwa pansu pa mbale unali thupi Lake lonyemedwa, limene Ayuda sangathe kufotokoza panobe chifukwa chimene iwo amachitira izo. Mukuona? Ndipo zinthu zina zonsezi zinkamuyimira Iye.

193 Tsopano, ndiye, Iye powonekera, ife tikuona tsopano zipembedzo zonse ndi tizikhulupiriro zasiyidwa mmbuyo; pakuti Iye ndi Mawu angwiro, osasinthika a Mulungu, amene ali mkate wopanda chotupitsa, Yohane Woyera 1. Izo nzoona, Iye ndi Mkate wopanda chotupitsa. Chotero pamene muwonjezera *ichi* kapena muwonjezera *icho*, ndi chotupitsa chowonjezeredwa kwa Icho chimene chinaperekedwa kale kwa inu.

194 Yang’anani apa. Ndi chiyani chimene chikupha mtundu lero? Iwo amatenga ndi kusakaniza zinthu. Ndipo pamene inu musakaniza izo, inu mumazipha izo. “Oh, izo zimawoneka zokongola kwambiri.” Ndithudi! Chimanga cha haibridi: konifulekisi, ma phala onse amene amachokera ku chimanga. Chimanga cha haibridi: mapesi aakulu, akaso, otalika bwino, ndi makutu aakulu, chikuoneka bwino kawiri kuposa chinacho. Koma ndi imfa! Ngakhale sayansi inazipeza izo. Mukuona? Musazisakanize zimenezo, izo zikuphani inu.

195 Tsopano, apa, ndiroleni ine ndikuwonetseni inu. Tsiku lina ndinkathirira maluwa pa bwalo langa. Ndipo donayo anali ndi maluwa ena a haibridi amene anali mu m’phika

waung'ono apa, kapena chobzala chaching'ono pambali pa nyumbayo. Ife tinkayenera tizithirira zinthu zimenezo katatu pa sabata, kapena kanayi, apo ayi zifa. Ndipo apo panayima mbewu yapachiyambi kunja pabwalo. Sikunagwe mvula kwa miyezi sikisi, kowuma basi... Ngati mvula ingagwe, mu maminiti khumi mukhoza kuwomba fumbi. Koma kanthu kakang'ono ako katagona kunja uko, kokongola ndi kowala basi kuposa momwe chinaliri chahaibridi ndi madzi onse. Inu mukachotsa madzi amenewo pa icho, icho chifa. Koma kodi icho chinatenga madzi ake kuti? Ndipo chinthu china, iwe umayenera kumapita kukapopera izo tsiku lililonse kapena awiri, kuti muthamangitse nsabwe pa izo. Iwo satero, nsabwe zidya icho, icho ndi chanthete kwambiri komanso chofewa. Koma palibe nsabwe imene ingafike pa chapachiyambi. Ayi, ayi! Iyo idzakwawira kwa iye ndi kukwawira kutali. Icho ndi chapachiyambi! Mukuona chimene haibridi yachita?

¹⁹⁶ Ndicho chinthu chomwecho mu mpingo. Iwo akuyesetsa kusakaniza chipembedzo ndi Mawu, kuti apange a... kuyesetsa kuti awapangitse Mawu kunena chimene chipembedzo chikunena. Ndipo pamene inu muchita zimenezo, inu muyenera kuwapopera iwo, ndi kuwasasatitsa iwo, ndi—ndi kuwapatsa iwo nyenyezi zagolide kuti azibwera ku Sande sukulu, ndi china chirichonse. Uko nkulondola. Pamene, Mkhristu weniweni, wobadwa mwatsopano, wobadwa ndi Mawu a Mulungu, iye ndi wolimba. Ameneyo ndi inuyo. Nsabwe ndi zinthu za mdziko sizimamuvutitsa iye. Iye ndi mphungu, iyo imawulukira kutali kudutsa zimenezo. Mwaona, amawulukira mmwamba. Mukuona? Ndi zoon. Palibe...

¹⁹⁷ Zindikirani. Tsopano, tikuyenera kumvetsetsa kuti apa, chipembedzo, tizikhulupiriro, ndi chirichonse chimene chawonjezedwa mu mkate wa chotupitsa sichingasakanikirane ndi mkate wopanda chotupitsawo. Ndipo Baibulo likuwonetseratu apa mu mwambo, wa kulowa mu kupembedza, kuti palibe chopanda chotupitsa chimene chingadyedwe ndi inu, ndipo Mulungu nkuchilandira icho.

¹⁹⁸ Inu mukuti, “Ndine wa Methodisti.” Pomwepo inu mukufa! “Ndine wa Pentekoste.” Inu mukufa!

¹⁹⁹ Ndine wa Khristu. Uko nkulondola. Inu mukuyenera kuyima pa chinachake. Uko nkulondola. Ndinu—inu mwayima pa chinachake.

²⁰⁰ Churchill ananenapo, anakweza mmwamba zala ziwiri ndipo anati, “Ife tiri ndi chigonjetso.” Ndipo England anayima pa icho, iwo anamukhulupirira Churchill.

²⁰¹ Ndipo khulupirirani izo kapena ayi, mmawa uno, inu mukuyima pa chinachake. Pali chinthu chimodzi chokha chimene inu mungakhalire nacho moyo ndi kuyimapo, ndipo ndicho Khristu, Mawu. Zoon!

²⁰² Zindikirani, palibe chirichonse mu Baibulo chimene chimayimira zipembedzo koma Babeloni. Ndipo Babeloni anak hazikitsidwa ndi Nimrodi, ndipo Nimrodi anali chigawenga. Ndipo iye anali ndi gulu la akazi mmenemo, ankayenera kukhala mfumukazi zake, amene anali aneneri aakazi. Iwo mpaka amaganiza kuti Balaamu wokalamba anachokera ku gawo limenelo, iwo anali ndi mizu ndi zina zotero. Iwo ankapembedza, inu mukudziwa (ambiri a inu ophunzira amene mukuwerenga *Two Babylons* ya Hislop, ndi ena otero, ndi mbiriyakale ya mpingo), ndi momwe iwo—iwo anachitira. Ndipo iwo anali ndi akazi amene ankachita *ichi*, ndi akazi . . . mulungu wamkazi, ndi chirichonse, ndipo icho chinali chipembedzo chokakamiza. Aliyense, mzinda uliwonse wozungulira Babeloni umakakamizidwa kubwera ku Babeloni kudzapembedza pansu pa Nimrodi pa nsanjapo. Mukuona? Uko nkulondola. Iwo anakakamizika kuti achite zimenezo, ku Babulo. Kumeneko ndi kumene chisokonezo chinabwera.

²⁰³ Ndipo ndicho ndendende chimene mpingo uli lero, “Ngati simupita ku Sande sukulu, ngati simuchita *ichi*, ndipo ndikuyenera kukuchitani ganyu kuti muchite *ichi* ndi kuchita *ichi* ndi kuchita *icho*, mwachoka pa chithunzicho.”

²⁰⁴ Kunja uko mu Tucson, akumvetsera mmawa uno, ine nthawi ina ndinkadabwa . . . Nthawi zonse ndimawakakamiza anthu, “Pitani ku tchalitchi, ziribe kanthu kumene mukupita.” Ndipo ine ndinawaonapo anthu akukhala ngati akubwerera mmbuyo, ndi kumapita njira *iyi*. Ndipo ine ndinaganiza, “Vuto ndi chiyani?”

²⁰⁵ Ndinapita kwa ena a iwo, “Tsiku loyamba ukafika kumeneko, iwo amakupeza iwe, ‘Jowinani mpingo wathu.’ Ngati suchita zimenezo, iwe sumalandiridwa.” Mukuona? Mukuona? Ndi chinthu chokakamiza, icho chimakakamizidwa pa inu, mwaona, ndipo uyo ndi Babeloni. Koma mwa Khristu, inu mumabweramo mwa kusankha; osati mokakamiza, mtima wako umakukokera iwe mkati.

²⁰⁶ Mulungu sanayike Dzina Lake pamene mu Babeloni. Mwatcheru tsopano. Iye sangayike Dzina Lake mu Babeloni, mipingo. Oh, iwo, *ivo* anayika Dzina Lake mmenemo, koma Iye sanatero. Ayi.

²⁰⁷ Inu mukuti, “Chabwino, tsopano, M’bale Branham!” Dikirani, dikirani, ingokhalani chete miniti yokha. Munandipempha ine kuti ndikhale motalika pang’ono. Kodi simukuona? Tsopano zindikirani, *ivo* anayika Dzina Lake mmenemo, koma Iye sanatero.

²⁰⁸ Tsopano, Iye anati, “Malo amene ine nditi ndidzakumane nawe ndi kulandira nsembe yako ndi kumene ine ndasankha kuyika Dzina Langa. Inu mubwere pa chipata ichi, khomo ili

pamene ine ndasankha kuyikapo Dzina Langa. Kumeneko ndi kumene inu muzibwera.”

²⁰⁹ Chabwino, iwo anayika, “Uwu ndi mpingo wa Khristu.” Ngati pali chirichonse chimene chiri cholakwika mu kulengeza kumeneko, chinasiya mawu amodzi: “wotsutsa.” Uh-huh, zonse zimene Iye ankaphunzitsa, iwo samagwirizana nazo Izo. Afarisi amakono.

²¹⁰ Koma tikuyenera kupeza pamene Iye anayika Dzina Lake, pakuti Mmenemo ndi mmene muli chipata Chake choperekedwa chokhacho. Amen! Ulemelero! Penyani! Kodi Iye anayika kuti Dzina Lake? Mwa Mwana Wake.

²¹¹ “Oh,” inu mukuti, “tsopano dikirani miniti, M’bale Branham. Ameneyo anali Mwana, osati Atate.”

²¹² Mwana nthawizonse amatenga dzina la abambo ake mu chochitika chirichonse. Ine ndinabwera pa dziko lino mu dzina la Branham chifukwa dzina la abambo anga linali Branham.

²¹³ Yesu anati, “Ine ndinadza mu Dzina la Atate Anga, ndipo inu simunandilandire Ine.” Inu mukufuna Lemba pa izo? Yohane Woyera 5:43. Mukuona? “Ine—Ine ndinadza mu Dzina la Atate Anga, ndipo inu simunandilandire Ine.” Ndiye Atate anayika Dzina Lake Lomwe, limene ndi “Yesu,” mwa Mwana. Ndipo Iye ndi Njira, Iye ndi Khomo, Iye ndi Nyumba, Iye ndi kumene Mulungu anasankha kuti ayikepo Dzina Lake. Mulungu sanayikepo Dzina Lake mwa ine, Iye sanaliyike Ilo mu mpingo, Iye sanaliike Ilo mu Methodisti, Baptisti, Katolika, koma Iye analiika Ilo mwa Khristu, Emanuele Wodzozedwayo.

²¹⁴ Ndipo Dzinalo liri mu Mawu chifukwa Iye *ndi* Mawu. Amen! Kodi Iye ndi chiyani ndiye? Mawu otanthauziridwa ndi kuwonetseredwa kwa Dzina la Mulungu. Nzosadabwitsa. “Thupi ndi mwazi sizinaulule ichi kwa iwe, koma Atate Anga amene ali Kumwamba awulula izi kwa iwe, Chimene Ine ndiri. Ndipo pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo malo Anga opembedzerapo, ndipo zipata za gehena sizingagwedezere Iwo pansu.” Amen! O Mpingo wamoyo wa Mulungu, imani pa maziko olimba pa Yesu Khristu yekha. Inu mukhoza kuyimba nyimboyo, koma ngati simuli pa Khristu Mawu, ndinu mchenga wosesereka, wopanda mphamvu. “Koma pa Thanthwe ili,” Khristu, “Mawu Anga.”

²¹⁵ Iye anamangapo uthenga wa Chilutera ndipo iwo anawupanga iwo chipembedzo. Iwo unakula, chopondapo mapazi. Kenako Iye anakula mpaka mu gawo la mwendo, Amethodisti, ndi zina zotero. Kumeneko ndi kumene Iye anamanga Mpingo Wake, pa Mawu Ake! Tsopano, Iye si zonse phazi kapena ntchafu yonse, Iye ndi thupi; ndipo tsopano ndi gawo lovindikirira. Kodi inu munazindikira mu mapiramidi? Chimene, ine sindimalalikira chipembedzo cha piramidi, tsopano.

²¹⁶ Koma Baibulo limene linayamba lalembedwapo, linalembedwa mmwamba, zo- . . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Kodi inu munazindikira zimenezo? Ilo limayamba ndi namwali, chinthu choyamba mu zodiyaiki. Chinthu chomaliza ndi Leo mkango. Iye anabwera poyamba mwa namwali, Iye akudza motsatira ngati Mkango wa fuko la Yuda. Zisanachitike zimenezo, m’badwo wa khansa, nsomba yopingasa, mibadwo ina yonseyo. Ngati ife tikanakhala ndi nthawi yodutsamo; chimene ife tikakhala nayo, ku kachisi.

²¹⁷ Ndipo pira- . . . piramidi pokhala maziko amenewo, mpaka kukafika mu chipinda cha mfumu. Ndipo basi musanagunde khoma lachiseveni, pali thabwa laling’ono lolozera pameneo, kumene wa mthenga amatulukirako kudzakutengerani inu kwa mfumu. (Wa mthenga, Yohane M’batizi, amene anamulozetsa, kwa Mfumu.) Koma Mwalawapamutu unakanidwa. Ndipo iwo sakudziwa, Mwala wa Sikono, kapena chirichonse chimene iwo uli, iwo sakudziwa kumene iwo uli, chifukwa iwo ndi mwala wokanidwa. Koma umenewo ndi mwala umene umamalizitsa chinthu chonsecho, umene umapanga icho kukhala piramidi kudzera mu mibadwo seveni yathunthu ya mpingo. Onjezerani chisomo, onjezerani *ichi*, onjezerani *ichi*, pali zowonjezera seveni, chotsiriza ndi Khristu. Onjezerani *ichi* ku chikondi chanu, onjezerani chisomo, pa chisomo chanu onjezerani chinachake, ndi chinachake, mpaka izo zitafika kwa Khristu ndi Mwalawapamutu, “Ndipo Ine ndine Khomo.”

²¹⁸ Tsopano, mwana nthawizonse amabwera mu dzina la abambo ake. Mwana aliyense amabwera mu dzina la abambo ake. Ndipo Yesu anati, “Ine ndinabwera mu Dzina la Atate Anga.” Ndiye Dzina la Atate ndi chiyani? Dzina la Mwana ndi chiyani? Ndipo Iye anati, “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine.” Eya, Iye wabwera mu mawonekedwe a Mzimu Woyera, Dzinalo ndi Yesu. Ndi chifukwa chimene iwo ankapembedza, “O Yesu!” Mukuona? Mukuona? Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera: Ndi Ambuze Yesu Khristu. Ndizo zonse. “Ine ndabwera mu Dzina la Atate Anga, ndipo inu simunandilandire Ine.”

²¹⁹ Tsopano, kumbukirani, Iye anawonjezeranso apa ndi kutichenjeza ife, “wina akadzabwera,” chipembedzo, kachikhulupiriro. “Iwo adzabwera mu dzina lawo ndipo inu mudzawalandira iwo. Inu simudzandilandira Ine, Mawu ovomeredwa ndi kutsimikiziridwa pamaso panu.”

²²⁰ Monga Iye anali nthawi imeneyo, chomwechonso Iye ali lero. Musaphonye zimenezo, anthu kudutsa fuko lino! “Wina adzabwera, mpingo, ndipo inu mudzakhulupirira izo, chifukwa inu mukhoza kungochita mwanjira iliyonse. Ine sindidzachitsimikizira icho.” Iye sanatsimikizire konse (pa nthawi iliyonse, nkomwe) chirichonse (mu mpingo uliwonse) kunja kwa Uthenga umene unaperekedwa: Wa

Luther, kulungamitsidwa; Wesley, kuyeretsedwa; Pentekoste, kubwezeretsa kwa mphatso. Zitatha...Ndipo mwamsanga pamene iwo anapanga chipembedzo mwa icho, apo icho chinafa. Fufuzani Malemba.

221 Koma Iye anati, “Ine ndidzasankha malo oti ndidzayikepo Dzina Langa.” Ndipo Dzinalo linali Yesu. Ndipo Yesu ndi Mawu, Yohane Woyera 1. Nkulondola uko? Amenewo ndiwo malo opembedzerapo, mwa Khristu Mawu. “Ine ndabwera mu Dzina la Atate Anga.”

222 Mneneri anati, “Dzina Lake lidzatchedwa Emanuele.” Ameneyo ndi Mateyu 1:23, ngati inu mukufuna kulemba izo. Yesu, Yehova, Mpulumutsi.

223 Tsopano, ndime ya 5 ikuwonetsera kuti Iye ndi Khomo. Pakali pano, maumboni ena ambiri osawoneka, Chipata ichi, ndi Dzina, ndipo malo akhoza kutsimikiziridwa kuti pali malo amodzi okha amene Mulungu amakumana ndi munthu kuti azimupembedza, ndipo ndi pamene iye akhala mwa Khristu.

224 Tsopano, tsopano funso ndilakuti, “Kodi ife timalowa bwanji mwa Iye?” Tsopano, izi zikhoza kutsina pang’ono pokha; koma, inu mukudziwa, monga kumwa mankhwala, ngati iwo sakudwalitsani inu, iwo sakuchitirani inu ubwino uliwonse. Mukuona?

225 Tsopano, Achilutera ankafuna kuti apite njira imodzi, pojowina mpingo wa Lutheran. Amethodisti ankafuna kuti alowe pofuula. Achipentekoste ankafuna kuti alowe poyankhula mmalirime. Izo si zimenezobe! Mukuona? Ayi, zimenezo ndi mphatso, zina zotero. Koma Akorinto Woyamba 12 amati, “Mwa Mzimu umodzi.” Mzimu wa Mulungu, umene uli wopereka Moyo kwa Mawu (Mbewu), kuti utsimikizire Mbewu imeneyo ya nyengo imeneyo. Mukuona?

226 Apa pali mbewu ya m’badwo wa Methodisti ili pamenepo, zinatengera Mzimu Woyera kuti upangitse mbewu imeneyo kukhala yamoyo ndi yoyera...kuwuyeretsa mpingo mwa kuyeretsedwa; Luther sanalalikire zimenezo, chifukwa iye samadziwa zimenezo. Achipentekoste ankafuna kuyankhula mmalirime kwa kubwezeretsa kwa mphatso. Aliyense amanena, “Ndi Ichu! Ndi Ichu!” Mukuona?

227 “Koma mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi,” ndipo Thupi limenelo ndi banja, banja la Mulungu. Ndipo ndiyo Nyumba ya Mulungu, ndipo Nyumba ya Mulungu ndi Dzina la Yesu Khristu. “Dzina la Ambuye ndi Nsanja yamphamvu, olungama amathawiramo mwa Iyo ndipo amatetezeka.”

228 Tsopano, inu mubweramo bwanji ndi udindo? Kodi cheke chanu chilandiridwa bwanji ponena kuti, “Chinalipidwa ku dongosolo la—la M’busa, Dokotala, Mtumiki”? Mukuona?

Mukuona? Inu mukhoza kukhala m'busa, dokotala, mtumiki. Koma *dzina* la Ambuye ndi “Yesu Khristu.” Mukuona?

229 “Ine ndasankha kuyikapo Dzina Langa pakhomo la nyumba Yanga yopembedzeramo, pakuti banja Langa lidzasonkhanitsidwa mmenemo pansi pa Magazi; monga zinali ku Igupto, chirichonse chakunja chinafa. Ndipo mmenemo mulibe mkate wachotupitsa! Mulibemo kusakaniza kwa chipembedzo mwa Iwo paliponse, nyumba Yanga! Ana Anga, obadwa ndi majini Anga!” Ameni! Ulemelero kwa Mulungu! “Majini anga ali mwa iwo! Mai. . . Ine ndayika Mawu Anga mwa iwo. Ndidzawalemba iwo pa magome a mitima yawo. Limenelo ndi banja Langa, banja la Thupi la Yesu Khristu; banja. Ndipo khomo ili inu mudzalowamo, osati Methodisti, Baptisti, kapena Pentekoste, koma pakhomo limene Ine ndayikapo Dzina Langa.” Izo si Methodisti. Dzina la Mulungu si Methodisti. Dzina la Mulungu si Chipentekoste. Dzina la Mulungu si Baptisti. Dzina la Mulungu si Katolika. Khalani kunja kwa zitsekozo ndiye. Mukuona? Mukuona? Mukuona?

230 “Koma pamalo amene ndasankha kuyikapo Dzina Langa.” Tsopano, palibepo malo ena mu Baibulo operekedwa pamene Mulungu anayamba wayikapo Dzina Lake, kokha mwa Yesu Khristu, pakuti Iye ndi Mwana wa Mulungu akutenga Dzina la Mulungu, ndi Dzina la umunthu la Mulungu. “Ndipo palibepo dzina lina loperekedwa pansi pa Kumwamba limene inu mukuyenera kupulumutsidwa nalo.” Ine sindikusamala, Methodisti, Baptisti, Presbateria, makatekisimu, kapena chirichonse chimene inu mukufuna kuchita; kokha kupyolera mu Dzina la Yesu Khristu kumene bondo lililonse lidzagwada ndipo lirime lililonse lidzavomereza kwa ilo, Iye kukhala Ambuye. Umo ndi momwe mumalowera.

231 Ndipo ngati inu munangobatizidwa mmadzi molondola—molondola, ndiyeno nkukana Mawu, ndiye ndinu apathengo; kubadwa kwanu sikunali kolondola. Inu mumadzinenera kuti inu munamukhulupirira Iye apo, ndipo inu mukumukana Iye.

232 Ndingakane bwanji banja langa? Pamene. . . Ine ndingamukane bwanji Charles Branham kukhala bambo wanga? Kuyezetsa magazi pachitseko kumawonetsera izo. Uhuh.

233 Zochita zanga, ndi kutsimikizira kwa Mawu a Mulungu mmoyo wanga zimawonetsera ngati ndiri mwana wa Mulungu kapena ayi. Tsopano, alipo malo okhawo a Mulungu. Mukuona zimenezo? Malo okhawo amene Mulungu angalandire nsembe yanu (ine sindikusamala momwe inu muliri woonamtima) ndi mwa Khristu.

234 Ndipo kumbukirani. . . Inu mukuti, “Chabwino, ine ndinakhulupirira; ine ndilowa, nanenso.” Kumbukirani, Baibulo limati. . . Inu mukuti, “Chabwino, Baibulo linati,

‘Aliyense amene akhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu, ndi wopulumutsidwa, adzapulumutsidwa.’”

²³⁵ Ilo limanena izo, koma kumbukirani kuti kwalembedwanso, kwalembedwanso, “Palibe munthu angamutchule Yesu Khristu, kokha mwa Mzimu Woyera.” Mukuona? Inu mukhoza kunena kuti “Iye ali,” koma Iye siali mpaka Mzimu Woyera Iwomwini, umene umapereka Moyo ku Mawu, utatsimikizira izo mwa kutsimikizira kuti ndinu mwana wa Mulungu. Amenewo ndiwo Malemba.

²³⁶ “Malo amene Ine ndinawasankha kuyikapo Dzina Langa. Inu simudzapembedza pa chipata china chirichonse, koma pa chipata chimene Ine ndiyakapo Dzina Langa; ndiye Ine ndidzakulandirani inu, inu muli m’banja Langa.”

²³⁷ Tsopano, banja la Mulungu limamvera ulamuliro wa Atate wa banja. “Ndipo Iye ndi Kalonga wa Mtendere, Mulungu Wamphamvu, Atate wosatha; ndipo ulamuliro Wake ndi ufumu sudzakhala ndi mathero, ulamuliro udzakhala pa mapewa Ake.” Ndipo Iye pokhala Wolamulira, Mfumu, Emanuele, Woyamba, Wotsiriza, Kalonga wa Mtendere, Mulungu Wamphamvuzonse, Atate wosatha, aliyense wa ana Ake amamvera Mawu aliwone momwe alamuliridwira chifukwa iwo ndi gawo la Iye.

²³⁸ Ife timakhala mnyumba yathu monga a Branham amakhalira. Inu mumakhala mnyumba mwanu, a Jones, monga a Jones amakhalira.

²³⁹ Ndipo Mnyumba ya Mulungu timakhala ndi Mawu a Mulungu ndi Aliyense wotuluka mkamwa mwa Mulungu; ndi china chirichonse, chinyengo, ife sitimumvera iye. Mukuona? “Inu muzidzadya mkate wopanda chotupitsa, m’badwo uliwone wa mpingo, monga momwe ine ndawuperekerwa Iwo kwa inu.” Koma musayesere kubwerera mmbuyo ndi kukabaira izo mu Izi, chifukwa izo zafika mu phesi. “Inu mudzatenga mafupa ndi zinthu zimene zatsalira pa nsembeyo ndi kuziwotcha!” Unapita, m’badwo wa mpingo unafa, unapitirira; ife tiri mu wina tsopano. Amen!

²⁴⁰ “Malo amene Ine ndasankha kuyikapo Dzina Langa.” Oh, mai! Akorinto Woyamba 12.

²⁴¹ Zindikirani, Aefeso 4:30.

...musawukwiyitse Mzimu woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo mpaka a... (chitsitsimutso chotsatira?)...mpaka tsiku la chiwombolo chanu.

...musawukwiyitse Mzimu woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.

²⁴² Tsopano zindikirani. Tiyeni tizigwiritse ntchito zimenezo ku phunziro lathu la Lemba. Ndiye kulibwino ife tipite;

ndikuganiza kuti ndikuwatopetsa anthu. Mukuona? [Wina akuti, “Ayi, inu simukutero, M’bale Branham.”—Mkonzi]. Tayang’anani apa, anthu akunyamuka ndi kumapita kwawo, inu mwaona, chotero iwo a—iwo akukaphika chakudya chamadzulo, ndi winawake amene iwo akufuna kuti akakumane naye. Iwo sanayembekezere kubwera kuno kudzamvetsera tsiku lonse. Mukuona? Koma, taonani, inu mukudziwa a . . .

²⁴³ [M’bale Ben Bryant ananena chinachake—Mkonzi]. Ben, oh, ine ndikuyenera kugwira ntchito pa iwe! Akudalitse iwe! Zikomo iwe, M’bale Ben. Ine ndimakukonda iwe, M’bale Ben.

²⁴⁴ Ngati inu mukanadziwa chimene mnyamata ameneyo anativutikira ife pa nkondo imeneyo; iye anawawombera onse mzidutswa, ndi kuphulitsidwa, ndi china chirichonse. Iye wakhalapo nawo moyo wa chirichonse, koma Mulungu wamudalitsa iye. Iye anakhala wona. Mkazi wake anamusiya iye, anathawa ndipo anakakwatiwanso, ndipo anatenga ana ake. Oh, mai, ine basi sindingathe kuganizira zimenezo.

²⁴⁵ Koma, mulimonse, Mulungu akudalitse iwe, Ben.

²⁴⁶ Iye ali pamenepo pakali pano wodzadza ndi tizidutswa ta zipolopolo, tikukanikiza mitsempha yake ndi china chirichonse. Chimene, inu mukuyenera kudziwa maziko a zinthu, inu mwaona. Mulungu amudalitse mnyamata ameneyo. Inde.

. . .umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.

²⁴⁷ Zindikirani! Tsopano, izi zikhoza kutsina pang’ono pokha, koma zindikirani. Musandisiye ine. Mungokumbukira.

²⁴⁸ Pamene Israeli nthawi yina anayang’ana pa chitseko chimenecho, ndi magazi amenewo pa chitseko, dzina (magazi, moyo), ndipo analowa pansu pa magazi amenewo, iwo sanatulukenso mpaka iwo atatuluka mu Igupto.

. . .musawukwiyitse Mzimu woyera wa Mulungu, umene mumalowamo ndipo osatulukanso mpaka tsiku limene mwawomboledwa. (Mukuona?)

²⁴⁹ Inu mukudziwa, Baibulo nthawizonse limakhala lolondola. Iye amayika Mawu Mmenemo, inu mukuyenera kuwayika Iwo kumene Iwo akupita, kuti muwapange Iwo, kupanga chithunzi chathunthu cha chiwombolo. Mukuona? Mukuona?

. . .musawukwiyitse Mzimu woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo mpaka chiwombolo chanu. (Mpaka inu mutawomboledwa.)

²⁵⁰ Inu munasindikizidwa mmenemo, inu muli pansu pa Magazi. Inu simukumatulukanso pano. Ndiyeno ndinu chiyani? Mwana wa Mulungu mu banja la Mulungu, wosindikizidwa ndi Mzimu Woyera. Mdierekezi sangakupezeni inu ngati akanati atero; pakuti munafa, gawo la mwamuna wanu wakale linafa; ndipo inu munayikidwa, ndipo moyo wanu unabisisidwa mwa Mulungu

kudzera mwa Khristu, ndi kusindikizidwa ndi Mzimu Woyera. Mukuona? Iye Akupezani bwanji inu? Inu mudzatuluka bwanji? Inu muli pamenepo! Ulemelero! Tsopano ine ndizisiya izo zokha; basi mokwanira kuti mudziwe chimene ndikunena.

²⁵¹ Ndiye chirengedwe chatsopano, osati ku chipembedzo koma ku Mawu. Ndinu cholengedwa cha Mawu. Chifukwa mwala wa maziko unayikidwa mwa inu maziko a dziko asanakhazikitsidwe, munasankhidwiratu kuti mudzakhale ana aamuna ndi aakazi a Mulungu.

²⁵² Ndipo pa ichi panadzabwera mwala pa mwala, mu m'badwo uliwonse, kuti udzatsimikizire Mawu amenewo amene akubwera, ndendende basi monga Yesu anachitira mu m'badwo Wake, umene uli Mwalawapamutu wa izo zonse. Mwa Iye munali m'badwo uliwonse. Mwa Yesu munali Mose. Mwa Yesu munali Davide. Mwa Yesu munali aneneri. Nkulondola uko? Tayang'anani pa Yosefe, anagulitsidwa kwa pafupifupi ndi zidutswa sarte za siliva, anaponyedwa mkati, anaganiziridwa kuti wafa, anadzachotsedwamo, anapita ndipo anadzakhala ku dzanja lamanja la Farao. Penyani, ndendende, Yesu anali... Yosefe anali mwa Yesu.

²⁵³ Ndipo pamene Iye anabwera, Iye anali chidzalo cha mafumu, aneneri (aleluya), umulungu mthupi unkakhala mwa Iye. Iye anabwera kuti adzawombole kuchokera mmenemo Mkwatibwi, Mbambande. Mbambande imene imanena kwa Satana kuti...

²⁵⁴ Pamene iye akuti, "Masiku a zozizwitsa anapita. Palibe chinthu ngati zinthu izi zimene mukuzinenazi."

²⁵⁵ "Pita kumbuyo kwanga, Satana." Mukuona? Mwaona, Mbambande itayima ndi kumatchinjuriza.

²⁵⁶ Nthawiyina Mwalawapamutu udzabwerera, mutu wa izo zonse, ndi kudzamulandira Mkwatibwi kwa Iyemwini; chimene mkazi amatengedwa kuchokera kwa mwamuna, gawo la mwamuna. Chirichonse... Nyongolosi za mwamuna zimakhala mwa mkazi, chimene chimampanga mkaziyo. Ndipo umo ndi momwe Mawu a Mulungu akukhalira mwa Mpingo, chimene chimawupanga Mpingo kukhala Mkwatibwi. Osati chipembedzo, icho ndi cha mdierekezi, chirichonse cha izo. Ine sindikuwatchula anthu ali mmenemo zimenezo; iwo ndi anthu osauka onyengedwa, monga Yesu ananenera, "Akhungu kutsogolera akhungu." Ndipo Iye sakanatha kuwaitanira iwo kunja.

²⁵⁷ Ndipo iwo anati, "Bwanji, unabadwa mu chigololo! Ndani akukuza iwe, pamenepo, kubwera kwa iwe? Ndi sukulu yanji, ndi mminare iti imene inakuzindikira iwe?" Anati, "Ife tiri naye Mose. Ife tikudziwa..."

²⁵⁸ Iye anati, "Ngati inu mukanamudziwa Mose, mukanandidziwa Ine."

²⁵⁹ Chifukwa Mose anamulemba Iye mu mabuku ake anayi, “Ambuye Mulungu wanu adzadzutsa Wopereka Mawu, kapena, Mneneri, wonga ine, ndipo amene sadzamumvera Mneneri ameneyo adzadulidwa kuchokera pakati pa anthu.” Ndizo zonse zimene ziripo kwa izo. Ndipo kodi Iye ndi chiyani? Mawu. Ndipo Iwo ndi chiyani? Musasiye chotupitsa chotsalira mu... chanu... musayike chotupitsa pakati pa Iwo. Musawonjezere kachikhulupiriro kalikonse, chipembedzo chirichonse, pakuti icho chaipitsidwa pamenepo, nsembe yanu yatha.

²⁶⁰ Tiyeni tifulumire tsopano, mwamsanga ndithu, kuti inu mupite mukadye.

²⁶¹ Zindikirani! Tsopano, ndiye, ndinu mwana wa Mulungu, mnyumba ya Mulungu, ndinu gawo la chuma cha Mulungu. Aroma 8:1, “Ndiye palibe kutsutsidwa kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu.” Pakuti iwo ndi akufa ku dziko, amoyo mwa Iye, ndipo akukhala mu tsiku lamakono lino, kuwapanga Mawu amene Mulungu wawagwiritsa ntchito iwo, kapena anawadzozeratu iwo, kuyika dzina lawo mu Bukhu la Mkwatibwi ili. Ndipo pamene Madzi abwera pa mbewu imeneyo imene ili mu mtima, amayiwukitsira iyo kwa Mkwatibwi wa Khristu. Oh, mai! Zangwiro basi momwe zingakhalire. Mu m’badwo uliwonse zakhala ziri chomwecho.

²⁶² Achilutera, pansu pa kulungamitsidwa, mapazi, anaukweza iwo monga choncho; Wesley, pansu pa kuyeretsedwa. Achipentekoste pansu pa mikonu, ntchito ndi zochita ndi zina zotero, anayenera kukhala Achikalvini... kapena amayenera kukhala a Chiarminiani, ankayenera kukhala amalalamulo. Koma tsopano ife tafika ku mutu, mwala wapamutu. “Chisomo! Chisomo!” Mwalawapamutu unalira.

²⁶³ Mwala wapamutu ukufuula chiyani? “Chisomo! Chisomo!” Wadutsa kuchoka ku imfa ndi kachikhulupiriro, wapita ku Mawu amoyo a Mulungu wamoyo. Dongosolo lokhalo loperekedwa ndi Mulungu ku m’badwo Wake, Ana Ake mu m’badwo wa Mawu amafulumizitsidwa ndi Mzimu ngati moto umene wayatsidwa kuchokera ku chinachake kuti ukhale wamoyo; ndipo akukhala tsopano mmalo amwambamwamba (mu nthawi yatsopano), amoyo kale ndipo omvera lonjezo lirilonse mu Mawu. Ndiye izo zimachita chiyani? Inu pokhala gawo la nyongolosi ya Mulungu, gawo la Mawu, anthu ena gawo la Mawu a Mulungu, titakhala limodzi, kuwonetsera Thupi lonse la Khristu, chifukwa palibe chotupitsa pakati panu. (Mukuona chimene Iye akuchikamba, M’bale Brown?) Popanda chotupitsa pakati panu, Mawu okha basi, atakhala mmalo amwambamwamba, pakhomo limene Iye anayikapo Dzina Lake: Khristu Yesu.

²⁶⁴ Popanda chotupitsa pakati panu, chimene chimabweretsa chidzalo chonse cha umulungu mwathupi mwa inu. Sakanachita

izo mu m'badwo wa Luther, sakanachita izo mu m'badwo wa Wesley, sakanachita izo mu m'badwo wa Pentekoste; koma mtsiku limene Mwana wa munthu adzawonekera, kuwululidwa, nabweretsanso Mpingo pamodzi ndi Umulungu wonse wa Mulungu pakati pa anthu Ake, kuwonetsera zizindikiro zooneka zomwezo, akudziwonetsera Yekha monga Iye anachitira pachiyambi pamene Iye ankawonetseredwa pa dziko mmawonekedwe a Mneneri-Mulungu. Oh! Ulemelero! Zinalonjezedwa ndi Malaki 4, zinalonjezedwa ndi Malemba ena onse. Kodi inu mumapembedza kuti? Nyumba ya Mulungu, mutakhala (mu nthawi yatsopano).

²⁶⁵ Tsopano, mwamsanga, tiyeni ife tiyang'ane mofulumira kwenikweni tsopano, ndipo kenako tizipitirira nazo... Mu maminiti teni ife tikhala titapita, Ambuye akalola.

²⁶⁶ Tsopano tiyeni tiyang'ane pa ena amene afulumizitsidwa kulowa mu nyumba ya Mulungu iyi, a m'badwo wawo.

²⁶⁷ Enoki! (Mu maminiti teni ife tidzipita, ngati mungapirire motalika chomwecho.) Penyani, Enoki anali Mawu amoyo a Mulungu a m'badwo wake, iye anali mneneri.

²⁶⁸ Mneneri ndi chonyezimiritsa Mulungu. Ndi angati amadziwa zimenezo? A—chonyezimiritsa sichidzinyezimiritsa chokha, a—chonyezimiritsa sichonyezimiritsidwacho. Pakuyenera kukhala chinachake chikugunda chonyezimiritsa—chonyezimiritsa kuti chinyezimiritse. Chotero mneneri ndi chotengera chosankhidwa cha Mulungu chimene sichinganyezimiritse kalikonse nkomwe koma iye amakhala pa mzere wolunjika ndi kunyezimira kumeneko, Mulungu, kuti anyezimiritse chifanizo cha Khristu, Mawu. Mwaona, palibe china chirichonse chingachite zimenezo. Inu ndi chonyezimiritsa, ndi chifukwa chake mneneri ankayenera kudya kabukhu. Ndi chifukwa chake iye ankayenera kudya mpukutuwo. Iye ankayenera kunyezimiritsa Mawu amenewo a m'badwo umenewo. Inu mukumvetsa zimenezo?

²⁶⁹ Taonani Enoki, wonyezimiritsa wangwiro wa Mulungu. Pamene Mulungu anathana—*anathana* naye, Iye anangomusantha iye, namutengera iye mmwamba. Zimango zimene iye anali atazinyezimiritsa zinadzakhala mphanvu ndi Mzimu, ndipo zinamutengera iye mmwamba.

²⁷⁰ Chimodzimodzi mu masiku a Eliya. Eliya, ngakhale mpaka mafupa ake, kumene chinyezimiritsa chimenecho... Chonyezimiritsa cha Mulungu mu thupi lake chikuwonetseredwa Mawu a Mulungu. Iwo anamuika munthu wakufa, iye anauka ku moyo kachiwiri. Ife ndife mnofu ndi fupa la Iye, pokhapokha ngati tiri Mkwatibwi wa Khristu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Chabwino. Iye anatifera ife, ndipo ife tinafa kwa ifeeni ndipo tinayikidwa mmanda mu Dzina Lake, kuti ife “sitidzakhalsano a dziko lapansi, koma mwa Iye,” amene banja lonse la Kumwamba limatchedwa Yesu Khristu.

Ameneyo ndi Aefeso 1:21. Kwa zonse ziwiri Kumwamba... banja la Kumwamba. Kodi banja la Kumwamba limatchedwa chiyani? Yesu. Kodi banja padziko lapansi limatchedwa chiyani? Chabwino, imeneyo ndiyo nyumba ya Mulungu kumene kuli Magazi. Nkulondola uko? Ndiro khomo, ndicho chipata, ndiwo malo amene Iye anayikapo Dzina Lake, ndipo Mawu anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu. Ndi Mawu akunyezimiritsa ndi kuwuyatsa m'badwo umene inu mukukhalamo. Ndicho chimene Iye anali, ndicho chimene Mose anali, ndicho chimene Yakobo anali, ndicho chimene ena onsewo anali, kuwayatsa Mawu a Mulungu amenewo, chonyezimiritsa chimene Mulungu ankadzinyezimiritsa Iyemwini. Ndipo anadzabwera ku chifaniziro changwiwo chimenecho cha Mulungu, Yesu Khristu, Mbambande ya Mulungu, Amene anakanthidwa kuti Iye akhoze kuwatenga ena onsewo kukhala Mkwatibwi amene wakhala zonyezimiritsa.

²⁷¹ Mose anali mwa Iye. Yoswa anali mwa Iye. Ndipo ngati inu muli mwa Iye, inu munali mwa Iye maziko a dziko asanakhazikitsidwe, banja la Mulungu; inu munavutika ndi Iye, inu munafa ndi Iye, inu munapita pa mtanda ndi Iye, inu munauka ndi Iye; ndipo tsopano inu mukadali ndi Iyeyo, mutakhala mmalo Ammwambamwamba, mukunyezimiritsa Uthenga wa m'badwo ku dziko, Kuwala kwa dziko. "Inu ndinu Kuwala kwa dziko lapansi," koma ngati iko kukubisidwa ndi dengu lophimba la chipembedzo, iwo adzakuwona bwanji Iko? Chifukwa cha miyambo yanu, inu mukukupangitsa Kuwala kukhala kopanda ntchito! Poyesera... Inu azipembedzo, mukuyesera kukuyika Kuwalako kutali ndi mpingo wanu; inu simudzalowa, komanso simudzawalola iwo. Amen.

²⁷² Tiyeni tingoyima. Mai, ine ndiri ndi zochuluka kwambiri apa. Ife—ife tikanatha kumapitirira... Oh, mai! Maminiti asanu ife tiri nawo.

²⁷³ Inu mukuona kuti khomolo ndi ndani? Kodi Mulungu anayika pati Dzina Lake? Mwa Yesu. Inu mumalowamo bwanji mu Dzina Lake? Inu mumalowamo bwanji mmenemo? Pobatizidwira mmenemo! Motani? Ndi madzi? Ndi Mzimu! "Ambuye mmodzi, chikhulupiriro chimodzi, ubatizo umodzi." Umenewo ndi ubatizo wa Mzimu Woyera.

²⁷⁴ Ubatizo wa mmadzi umangokuyikani inu mu chiyanjano ndi anthu, kuti inu mwazindikira kuti mwamulandira Khristu. Ndicho Choonadi. Koma ndi ubatizo wa Mzimu. Ine ndikhoza kutchula Dzina la Yesu pa inu ndi kukubatizani inu, izo sizipanga izo kukhala chomwecho.

²⁷⁵ Koma pamene kamodzi Mzimu Woyera uwo kwenikweni... Mawu enieni abwera mwa inu (Mawu, Yesu), ndiye, m'bale, Uthenga sumakhala chinsinsi kwa inu pamenepo; inu

mukuwudziwa Iwo, m'bale, Iwo wonse wawala pamaso panu. Aleluya! Matamando akhale kwa Mulungu! Amen!

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine,
Nandigulira changa chipu- . . .

Wokonedwa Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu muwachize anthu awa, Ambuye, ndi kumupanga aliyense wa iwo kukhala bwino. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

276 Oh! Chikondi! Oh!

Chiyambireni, mwa chikhulupiro ine
ndinawona mtsinje umenewo
Mabala anu oyenderera amapereka,
(Kuchokera ku Mbambande ija.)
Chikondi chowombola chakhala mfundo
yanga,

277 Inu mungathe bwanji. . .? Mulungu ndi Chikondi. "Iye amene amakonda ndi wa Mulungu," Chaumulungu, chikondi choyera, osati chikondi chauve; choyera, changwiwo, chikondi choyera, chikondi cha Mulungu Mawu. "Malamulo anu ndawabisa mu mtima mwanga, kuti ndisakuchimwireni Inu," oh, mai, Davide uja akufuula. Kodi Iye si wodabwitsa? Kodi inu simukumukonda Iye?

278 Tsopano, ilipo Njira, Njira yangwiwo, yoyera, malo okhawo okumaniranapo amene Mulungu ati adzakumane ndi inu. Osati chifukwa choti mumati, "Mulungu, tsopano, ndine wa Methodist wabwino. Ndine wa Baptist wabwino. Ndine wa Pentekoste wabwino." Ayi! Chifukwa chakuti inu muli mwa Yesu Mawu, gawo la Mawu limene likuwonetseredwa mpaka lero, Uthenga wa tsiku *lino*; osati wa Luther, wa Wesley, wa Pentekoste; koma Yesu wanu, chinyezimiritso, chimene chabwera mu *ichi*. Inu simungabwerere kwa *izo*, uko ndi kuwonjezera chotupitsa ku Mkate wanu woyera, kuti, "Munthu adzakhala moyo ndi Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu, mu nyengo Yake."

279 O bwerani, Ambuye Yesu, Mwalawapamutu waukulu. Tayang'anani ali uko, fumbi la Achilutera awo amene anafa mmbuyo pansu pa kufera; yang'anani pa Amethodisti awo.

280 Achipentekoste amenewo ndi ena otero, akubwera tsopano, kupsyinjika kwenikweni uko kumene kunatulukira.

281 Inu a Assemblies of God munapita ndipo munakapanga bungwe, pamene n'chinthu chomwecho chimene Mulungu anakutulutsanimu inu, inu munabwerera ngati nkhumba ku matope ake.

282 Inu a Oneness, United, J.C. wakale wa . . . Pentecostal Assemblies of Jesus Christ. Umodzi wa achikuda, ndipo munadzilekanitsa nokha chifukwa cha tsankho. Inu amene

munachita zimenezo, ndipo kenako munadzigwirizanitsa nokha ndi kudziticha izo “Ogwirizana.” Ndipo kenako anapanga bungwe, ndipo anakangana nawo a Assemblies: “Monga galu amatembenukira ku masanzi ake.” Ngati masanziwo anadwalitsa galuyo poyamba, kodi sangamudwalitse iye kachiwiri? Sinthani zakudya zanu kuchoka ku chipembedzo chanu kupita ku Mawu, ndi kumakhala moyo ndi Khristu. Manyazi pa inu!

Ndiri ndi Atate uko,
Ndiri ndi Atate uko,
Ndiri ndi Atate uko,
Kugombe linalo.

Tsiku lina lowala ndidzapita kukamuwona Iye,
Tsiku lina lowala . . . pita kukamuwona Iye,
Tsiku lina lowala ndidzapita kukamuwona Iye,
Kugombe linalo.

Oh, kodi uwo sudzakhala msonkhano
wosangalatsa!

Kodi uwo . . . (Mawu amapita ku Mawu!) . . .
msonkhano!

(Pamene Mkwatibwi apita mmwamba, Mawu
ndi Mawu.) . . . msonkhano wokondwerera!

Kugombe linalo.

Oh, tsiku lowala limenelo likhoza kukhala
mawa,

Tsiku lowala limenelo likhoza kukhala mawa,
Tsiku lowala limenelo likhoza kukhala mawa,
Kugombe linalo.

²⁸³ Inu mukuti, “Inu mukutanthauza izo, M’bale Branham?”

²⁸⁴ Inde, bwana! Pamene Achilutera a m’badwo umenewo, a Wesley a m’badwo wawo, achipentekoste a m’badwo wawo (owonawo, osati azipembedzo); Apentekoste, awo amene anawonjezera chotupitsa (chipembedzo chawo), anafa. Koma Mawu owona awa akusunthira chitsogolo, mwaona. Chimodzimidzi monga Yesu ananena, “Pa tsiku limenelo, inu mudzaziwa kuti Ine ndiri mwa Atate ndipo Atate ali mwa Ine, ndipo Ine mwa inu ndi inu mwa Ine.” Onsewo ndi Mawu!

Oh, kodi uwo sudzakhala msonkhano
wosangalatsa! (Pamene ana Ake
adzasonkhana pa chipata Chake.)

. . . msonkhano wasangalatsa!

Umenewo sudzakhala msonkhano
wosangalatsa!

Ku gombe linalo.

²⁸⁵ Tsopano, mpingo, ife tikuphunzitsa tsopano. Koma, kumbukirani, pamene inu muchoka pano, muyambe kuchokamo mu mankhusu tsopano; inu mukupita mu njere, koma

mukakhale mu Kukhalapo kwa Mwana. Musakawonjezere, zimene ine ndanena; musakachotsere, zimene ine ndanena. Chifukwa, ine ndimayankhula Choonadi monga momwe ine ndikudziwira Icho, monga Atate andipatsira ine. Mukuona? Musawonjezere kwa Icho, mungonena chimene ine ndanena.

²⁸⁶ Chinthu chake ndi chakuti, mukangowauza anthu kuti abwere adzawafune Ambuye Yesu. Ndiyeno inu eniake mukhale mu Kukhalapo Kwake komwe, kungopanga chikondi ndi Iye, “O Ambuye Yesu, Mwana wa Mulungu, ndimakukondani Inu. Ukonzeni mtima wanga, Ambuye. Muchotsemo nyansi zonse ndi chikondi cha mdziko, ndipo ndiloleni ine ndikhale woyera mu dziko lino pamaso Panu.”

²⁸⁷ Tiyeni tiweramitse mitu yathu ku pemphero. Tsopano, tiyeni tiwone, kodi ife tiri ndi aliyense wasankhidwa kuti atibalalitse mu pemphero? Kapena, ine nditero, ndiye. Mukhale olemekeza kwenikweni.

²⁸⁸ Wokonedwa Mulungu, ife tikukuthokozani Inu kuti tinali ndi chakudya chathu chauzimu. Ife tikukuthokozani Inu, Ambuye, kuti vitamini ya Mawu imawakulitsa ana a Mulungu. Iyo siyimaipitsa mtundu wina uliwonse wa khalidwe, kokha pa ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Chotero ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha Zimenezo. Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti ife tipindule nazo, kuti ife sitingokuthokozani kokha Inu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha Izi, koma mutilole tigwiritse ntchito mphamvu kuti tiyesere (mwa Chikondi) kuwakakamizira anthu kuti akhulupirire mwa Mulungu wathu; opulikira, ochimwa, akazi, amuna, anyamata, atsikana, mu m’badwo uno.

²⁸⁹ Powona, Ambuye, kuti zikhaliidwe zaubongo, m’badwo wamanjenje umene anthu akukhalamo, zikuwachotsa iwo mmalingaliro awo; kuti akakwaniritse ndendende chimene Malemba ananena ndi kulonjeza, zinthu zazikulu zowopsya zikanadzabwera pa dziko lapansi; monga dzombe, kuti likawazunze akazi amene amameta tsitsi lawo, ilo lidzakhala ndi tsitsi lalitali ngati la mkazi. Ndi zowoneka zowopsya zosiyanasiyana zimene iwo azidzakhoza kuziwona, Ambuye, mu chikhaliidwe cha ubongo, wozerezeka chimene iwo alimo, ndiyeno nkumafuula kufuna matanthwe ndi mapiri. Akazi amene azidzalera agalu ndi amphaka, ndipo osalera ana oti azikulemekezani Inu. Iwo amene munawapatsa ana ndipo iwo anatenga pakati, anawataya iwo mmisewu kuti azichita monga momwe iwo akufunira. Nzosadabwitsa Inu munati, Ambuye, pamene Inu munkapita pa mtanda, “Kenako iwo adzayamba kulilira matanthwe ndi mapiri kuti awagwere.”


²⁹⁰ Ife tikuwona china chirichonse chikuyenda mpaka nthawi ino. Ife tikuwona Malemba akuvomerezedwa, kutsimikiziridwa. Ndipo basi pamene ife tikuwawona Iwo, Ambuye, Inu ndi

maso athu omwe (akuwonetseredwa), tsiku lina kudzakhala Mkwatulo ndipo ife tidzawona kuwonetseredwa kwa Mawu amenewo, “Pakuti Mwana wa munthu adzadza mmitambo ya ulemelero, ndi Angelo Ake oyera ndi Iye, ndipo ife tidzakwatulidwa kukakumana ndi Iye mu mlengalenga.” Zidzatero nthawi imeneyo...Ife tikumva za izo tsopano, panthawiyo ife tidzaziwona izo ndi diso lathu lomwe.

²⁹¹ Mulole ife tidzapezeke mwa Iye, Ambuye, malo okhawo operekedwa. Ndipo Iye ndi Nsembe. Ife tikumubweretsa Iye, chimene ife tamva, Yesu Khristu, kulowa mu nyumba ya Mulungu mwa ubatizo wa Mzimu Woyera, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo kumeneko Nsembe yathu imalandiridwa ndipo ife timabweretsedwa mu banja; chifukwa, komabe posochera mdziko, ife tinadzozedwa ana aamuna ndi aakazi a Mulungu maziko a dziko asanakhazikitsidwe. Zikomo Inu chifukwa cha izo, Atate. Oh, aliyense angakhoze bwanji kutembenuka pa chinachake ngati chimenecho, pamene iwo anapeza Choonadi, kuti Mulungu anawasankha iwo kuchokera mdziko? Panali mamiliyoni otayika, tsiku limene ine ndinapululumutsidwa.

²⁹² O Mwanawankhosa wakufa, ine ndingakuthokozeni Inu chotani? Mtima wanga ungakhale wolemekeza mokwanira chotani pamaso pa Inu? Ndithandizeni ine, wokonedwa Mulungu, kuti ndizikhala moona. Athandizeni anthu anga kukhala owona. Ine ndikuwapempherera iwo, Ambuye, aliyense, kuti Inu mutero, Mulungu, mwanjira ina, ine sinditero...sindingadziwe motani...Ine sindikudziwa motani, basi momwe ndingapemphere, Ambuye; ndipo mwinamwake ine sindikupempha izo mwanjira yoyenera. Koma Inu mukhululukire umbuli wanga, Ambuye, ndipo mungoyang’ana pa mtima wanga. Ine ndikupemphera kuti pasakhale mmodzi wa iwo ati adzatayike, osati mmodzi wa iwo, Atate. Ine ndikuwatengera iwo, mmodzi aliyense, kwa Inu. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

Ndinkonda Iye, ine. . .

Ndipo ngati inu mumamukonda Iye, inu muzikondana wina ndi mzake. Gwiranani chanza wina ndi mzake. 

65-1128M Malo Okhawo Operekedwa Ndi Mulungu Opembedzerapo
Life Tabernacle
Shreveport, Louisiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org